

# CHIBVUMBULUTSO, MUTU FAIVI GAWO I



Zikomo kwambiri, M'bale Neville. Ambuye akudalitseni inu, m'bale wanga.

<sup>2</sup> Mmawa wabwino, abwenzi. Ndi wokondwa mmawa uno, mwayi, kapena mwayi wawukulu, ine nditero, kubwerera kuno ku kachisi kachiwiri ndi kukhala ndi nthawi iyi yopatulidwa kwa kupembedza kwathu kwa mmawa ndi chiyanjano pa Mawu a Ambuye. Ine ndikukhulupirira izo zinanenedwa nthawi ina, “Ndinasangalala pamene ananena kwa ife, ‘Tiyeni tipite ku nyumba ya Ambuye.’” Kuti tidzakhalenso ndi M'bale Neville kachiwiri, ndi abwenzi anga abwino ndi ofunika.

<sup>3</sup> Ndipo ine ndikuganiza ndi kozizirirapo pang'ono, kapena kotentherapo pang'ono kumbuyo uko. Ndipo ife tiri ndi, ndikuganiza, zokupizira zina zomwe mungakhoze kugwiritsa ntchito ndi manja anu *motere*. Ngati—ngati. . . ife tiri ndi zokupizira ngati inu muli ndi mota, kuti basi izipangitsa iyo kuyenda. Kapena, ife tinali nawo ambiri kuzungulira kuno, ine ndikuganiza iwo akadali nawo iwo. Ndikuwona ena akugwiritsa ntchito mabuku a nyimbo kapena zina. Ndipo ndi. . . chinthu chimodzi chimene ife tikuyesera kuti tikhalire ndi mautumiki, ndi kuwazemba malo awa amene ali—ali mtsogolo omwe ndi otentha. Ndiye ife tiri. . . Ndicho chifukwa ife tiri pano mmawa uno, kuti tiwalambalale malo amenewo. Ndipo chinthu chimodzi chokha chimene chingakhoze kuchita izo, ndiwo Magazi a Ambuye wathu Yesu Khristu amene amachita zimenezo.

<sup>4</sup> Ndipo ine ndinali wokondwa kwambiri nditamva mbiri yabwino ya Mpingo, momwe iwo ukupitira chitsogolo, kumapitirira ndi Ambuye, ndi momwe Mulungu akuchitira nanu inu mu mphatso zauzimu. Ndipo ine ndithudi ndiri wothokoza kwambiri kwa Mulungu chifukwa cha mitima yanu yowona yomwe Iye angakhoze kuchita nayo, ndi kudalira kuti Iye akusungani inu pakati pomwe pa Njira yowongoka ndi yopapatizayo, kuti inu musasunthire kumanja kapena kumanzere kwa Iyo.

<sup>5</sup> Ndipo ine ndikufuna kuti ndimuthokoze M'bale Colvin ndi mwana wake wamkazi, ine ndikukhulupirira izo zinali, amene anali kuno mphindi zingapo zapitazo amene anayimba nyimbo ija, *Kulibe Misozi Kumwamba*. Zimenezo ndizokongola. Ine ndithudi ndikuyamikira izo.

<sup>6</sup> Ndipo monga M'bale Neville ananenera za iye ndi ine zaka zapitazo, ndipo ine ndikhoza kunena izo zokhudza M'bale

Colvin, ife tadziwana wina ndi mzake kwa zaka. Ndipo kumumva iye akuyimba nyimbo zakale za Uthenga ndi kuwalera ana ake mu njira ya Ambuye, ndi zokondweretsa kwambiri ku mtima wanga. Zimandipangitsa ine kusangalala kudziwa kuti Mulungu akadali ndi anthu amene amamukonda Iye ndi kusamala za Iye. Ndipo ife tiri oyamikira chifukwa cha izo.

<sup>7</sup> Tsopano, chibwerereni ine, ndikumva kuti ambiri abatizidwa mu Chikhulupiriro, ndipo ndife okondwa kwambiri chifukwa cha zimenezo. Ine ndikumuwona mzanga wabwino, M'bale Elmer Gabehart kumbuyo uko. Ine ndamva kuti iye anabatizidwa kumene mu Chikhulupiriro, ndipo ine ndithudi ndiri woyamikira chifukwa cha izo. Izo zimapangitsa gulu lathu lakale lonse losaka ku Kentucky kutsala pang'ono kukonzekera, kungotenga malire pano lokha, sichoncho izo?

<sup>8</sup> Ine ndikukumbukira (Ndipo ine ndikudziwa kuti Rodney akundimvetsera ine kuchipinda chakumbuyo, ngati iye ali komwekobe, ndipo Charlie wakhala patsogolo panga.) pamene ife tinkakonda kupita kumusi kumeneko. Anyamata onse anakonda kuti, “Chabwino, ndi agologolo,” iwo ankatengako pang'ono owonjezera ngati angawapeze iwo. Ndipo ine ndinayamba kuyankhula nawo ndipo izo sizinali zolondola. Kotero tsopano iwo ali . . .gulu lonse liri pafupifupi lotembenuka kotero ine ndikuganiza ife tikungoyenera kupita ku chigawo chotsatira ndi kuwawongolera iwo kumeneko. Izo zikhala bwino.

<sup>9</sup> Kotero nthawi zina ndimayang'ana pansi, monga mtumiki aliyense, pansi pa njira yomwe inu mwayendamo, ndi kudabwa za—zinthu, kuti ngati—ngati inu mwafesa Mbewu.

<sup>10</sup> Inu . . . ambiri a inu mumamudziwa bwino Johnny Appleseed mu . . . waku America. Bwanji, panalinso a—mwamuna ku Sweden amene ankalingaliridwa chinachake chonga chimenecho, iye ankafesa maluwa. Ndipo iwo amati ndi chifukwa chake ali ndi maluwa okongola ambiri mu Sweden tsopano, ndipo chifukwa ankafesa mbewu zamaluwa, kulikonse kumene iye akanapeza gawo la nthaka lomwe mbewu zimenezo zingameremo. Iye anakonda maluwa choncho ankatotaya mbewuzo mozungulira. Iye anapita koma maluwa ake akadali moyo.

Ndipo kusiyana kumasiya kumbuyo kwathu  
Mphondero mu mchenga wa nthawi;

Mphondero, kuti mwinamwake winawake,  
Pamene tikuyenda panjira yolemekezeka ya  
moyo,  
M'bale wokanidwa ndi wophwasuka,  
Pa kuwona, adzalimba mtima kachiwiri.

11 Ndipo ndicho chimene ife tonse timakonda kuwona, kuti chinachake chimene ife tachita icho zidzapangitsa ena kuti—kuti apindule ndi chimene ife tachita.

12 Masiku angapo apitawo ine ndinali nditakhala, ndikuyankhula kwa mzanga wamng'ono wokhulupirika kuno mu mzinda, dokotala wa mankhwala, Sam Adair. Ndipo iye anati, “Uli bwanji, Bill?”

13 Ndipo ine ndinati, “Oh, bwino kwambiri, ine ndikuganiza, Doc.” Ndinati; “Iweyo?”

14 Ndipo iye anati, “Oh, odwala ambiri.” Anati, “Ine ndinali ndi kuunika fifitini masanawa.”

15 Ine ndinati, “Chabwino, izo nzabwino bola ngati ziri zongowunika ndipo osapeza chirichonse cholakwika.” Ndinati, “Inu mukudziwa, a . . .” Tinayamba kukamba zokhudza pamene ife tinali anyamata. Ndipo ine ndinati, “Chabwino, Doc, ine sindikudziwa kuti ndikhala nthawi yayitali bwanji. Tonse tiri mu zaka za m'mafifite.”

Ndipo iye anati, “Ndi zowona zimenezo, Bill.”

16 Ndipo ine ndinati, “Koma zaka zonsezi, pafupifupi zaka sarte wani za utumiki tsopano, Ine ndasunga mtima wanga wokonzekera nthawi imeneyo pamene Iye adzabwera. Kotero ziribe kanthu kuti Iye abwera liti.”

Kotero iye anati, “Zimenezo ndi zowona.”

Ndinati, “Chinthu chosangalatsa kwambiri chimene ndiri nacho ndi kukhalira moyo anthu ena.”

17 Ndipo iye anati, “Ndi chimene moyo uli, zimapangitsa moyo kukhala weniweni, ndi pamene inu . . . osati zomwe mungathe kuchita kapena kukwaniritsa nokha, koma zomwe mungathe kuchitira ena.”

18 Mwaona, ndi pamene inu mukukhala moyo kwenikweni. Ndipo ngati pali wina pakati pathu amene sanachitepo zimenezo, kuyesetsa kuti amukhalire moyo wina, yesani kuchita izo, ndipo mungowona momwe moyo ungakhalire wochulukwa kwa inu pamene simudzakhala moyo pa zomwe mungadzipeze nokha mmoyo koma zomwe mungapatse wina mmoyo. Ndipo mudzapeza kuti ndi zodalitsidwa kwambiri kuposa chuma kapena chirichonse . . . chimene chingakhoze kuganiziridwa. Ndi zomwe mungachite kuti munthu wina apange zolemetsa za moyo . . . Chomwe, moyo pawokha ndi cholemetsa. Ndipo zidzapangitsa kuti zikhale zopepuka pang'ono kwa winawake. Inu simumadziwa chimwemwe chakecho pokhapokha mutayeserapo kamodzi, kuti muchite chinachake kwa winawake.

19 Ndiyeno izo zikundibweretsa ine ku kuganiza za zaka sarte wani (zikhala posachedwapa) za utumiki wa Ambuye. Ndipo ine ndikuganiza munthu aliyense amaganiza za nthawiyina pamene

iye ayenera kubwera ku msonkhano wake wotsiriza ndi kubwera ku ora lake lotsiriza, ndi kuyang'ana m'mbuyo mwa njirayo ndi kuwona zomwe zakwaniritsidwa, kuwona zomwe zachitika, “Kodi inu mwachitapo kanthu?” Ndipo ngati. . . ine ndangonena kumene, ndi zomwe inu mumachitira ena zomwe zimakhala zofunika.

<sup>20</sup> Nthawi zambiri ndimadabwa kuti zingadzakhale bwanji pamene ine ndifika kumapeto kwa njira yanga, chimene ife sitikudziwa kuti idzakhala nthawi yanji, palibe mmodzi wa ife. Kotero ine ndimagana za kuyang'ana m'mbuyo mwa mnjira imene ine ndadutsamo kupyola mu moyo ndipo ndawona mapiri osiyanasiyana ndi minga ndi miyala ndi malo olimba ndi kuyenda mofewa, ndi zomwe ine ndinachita mu nthawi zamtundu umenewo. Zonse zidzawonekera limodzi la masiku awa pa ora la kuchoka kwanga. Ndipo izo zidzachita zimenezo pa aliyense wa ife. Tonse tikhala otsimikiza za zimenezo, kuti zidzatero—zidzawonekera kwa aliyense pamene nthawi imeneyo idzafika.

<sup>21</sup> Ndipo izo zimandibweretsa ine kapena kundipangitsa ine kuti ndinene chinachake chimene ine ndikanakonda kuthawa kuposa kuchinena. Zikundipangitsa ine kunena chinachake chimene ine. . . Izo zimawuphwanyira pansi mtima wanga kuti ndinene izo, koma zomwe ine ndimanena ndimakakamizika kuti ndinene, pozindikira kuti izi zikujambulidwa ndipo dziko lidzazimva izo, koma ine ndasiya utumiki pa a—chifukwa chomwe ine ndikupepesa kuti ine ndiyenera kusiya. Ndipo mwinamwake ambiri a inu munazimva izo, ine ndikutseka ofesi yanga, ndi zina zotero, ndi kuchoka ku minda.

<sup>22</sup> Ine sindikudziwa komwe Ambuye wathu anganditsogolere ine, ndipo chimenecho ine ndiribe ulamuliro nacho, kapena chirichonse chimene Iye adzakhala nacho kuti ine ndichichite. Koma ine ndikuganiza kumapeto a ulendo kumene ine ndikuyenera kufika. Ndipo poyenda mu ulendo wa moyo ine ndapanga zolakwitsa zambiri zomwe ine ndikupepesa kuchokera mu mtima wanga, chifukwa, ine ndikuganiza, pokhala munthu ndi mu kufooka ndi zina zotero, zimamupangitsa munthu kuchita zinthu kapena kunena zinthu zimene. . . ndipo ngakhale kuchita zinthu zimene iwo sakanafuna kuchita mwanjira ina. Koma pokhala kufooka kwa munthu wokhalapo, bwanji, ife—ife tiri nazo nthawi zimenezo. Koma pali. . .

<sup>23</sup> Ngati pali chirichonse chomwe chakhala mu mtima mwanga choti nkuchichita, chinali kuti ndidzamve Mawu amenewo a Ambuye wathu Yesu pa mapeto a ulendo uwu, akuti, “Wachita bwino, mtumiki Wanga wabwino ndi wokhulupirika.” Ndipo nthawi zambiri ine ndanena kuti ine ndikanakonda ndikanakhala nditayima pamenepo pamene Iye anati, “Bwera kwa Ine”; koma ine ndinkafuna kumva Ilo likunena, “Wachita

bwino.” Kuti ine sindinamve Liwu, pachiyambi, likunena, “Idza kwa Ine,” kalelo mu nthawi za kulembedwa kwa Baibulo; koma ine ndikufuna kudzalimva Ilo likunena, “Wachita bwino.”

<sup>24</sup> Ndipo mwanjira ina nthawizonse ndinkafuna kuti ndikhale, ndipo zokhumba za mtima wanga kuti ndikhale, chinali mtumiki weniweni wa Yesu Khristu, Ambuye ndi Mpulumutsi wanga. Ine ndikufuna umboni wanga ukhale woyera, womveka bwino, kuti ine ndinayima, mu zolakwitsa zanga zonse komabe ndinamukonda Iye ndi mtima wanga wonse. Ndipo ine ndikuchita izo mmawa uno ndi mtima wanga wonse.

<sup>25</sup> Ndipo, chifukwa cha zimenezo, zikundikakamiza ine kunena kuti ndikusiya utumiki, ndi chifukwa chakuti pali chinachake chinawuka pakati pa anthu chimene chandipangitsa ine kuti ndichite izo, ndiko kuti, kuti ine ndachotsedwa ku bulangete langa la “mtumiki” kapena “m’bale” ndi kumatchedwa Yesu Khristu, ndi kuyitana kotero. . . ndipo izo zingandipangitse ine ngati wotsutsakhristu. Ndipo ine ndidzakomana naye Mulungu ngati wosiya ndisanakumane naye Iye ngati wotsutsakhristu kuti ndimuchotsepo Iye.

<sup>26</sup> Ine ndinamva za izo za—zaka zingapo zapitazo ndipo ine ndimaganiza kuti ndi nthabwala. Ndipo ine ndinakomana nawo abale angapo (omwe ine sindikuwona aliyense wa iwo mu msonkhano mmawa uno), awiri kapena atatu a iwo nthawi ina mu ulendo wokawedza, ndipo iwo anafikira kwa ine ndi mutu wakuti, “M’bale Branham, kodi inu sindinu Mesiya wodzozedwayo, Khristu?”

<sup>27</sup> Ndipo ine ndinayika mikono yanga mozungulira khosi la abale onse awiri, kapena, onse a iwo, ndipo ine ndinati, “Abale, monga momwe ine ndayesera kuti ndikhale wantchito woona wa Khristu, ine sindikanafuna kuti inu muzinena chinthu chotero monga chimenecho. Ndipo ngati izo zikananenedwa za ine, ndiye kuti ndidzachoka pa ntchitoyi ndi chikumbumtima choyera, ndipo inu amene mumachita zimenezo mudzakhala oyankhira kwa moyo uliwonse umene ndikanawupulumutsa pa nthawi imeneyo; mwaona, chifukwa chondichotsa ine kumunda.” Ndipo ine ndikuganiza kuti izo zathetsa zimenezo.

<sup>28</sup> Ndipo ine ndinamva izo kangapo konse. Koma sizinali choncho. Ndipo tsiku lina mu Canada m’bale anandiwonetsa ine tikiti yaying’ono ya chinthu chimene iye ananyamula mthumba mwake, inati “William Branham ndi Ambuye wathu,” kubatiza mu dzina la William Branham. Ndipo pang’ono. . . wofunika. . . Ngati akanakhala mdani, ngati akanakhala mdani wanga ine ndikanadziwa kuti inali nthabwala. Koma m’bale wofunika, wokonedwa anabwera kudzawulula machimo ake ndi zolakwa zake ndi kunena chikhulupiriro chake mwa ine monga kukhala Yesu Khristu.

<sup>29</sup> Ndipo ine ndiri nawo makalata kunyumba, ndi mafoni ochokera ku Chicago ndi malo osiyanasiyana, akundifunsa ine ngati ndimakhulupirira nthano zimenezo.

<sup>30</sup> Ndipo ine ndiri nayo mitundu yonse ya makalata amene abwera mu masiku angapo apitawa, ndi mafoni ochokera ku malo osiyanasiyana, kotero, kunena kuti ine ndinali Khristu. Abale, limenelo ndi bodza loopsa, lonyoza, lopanda umulungu la mdierekezi! Mukuona? Mukuona, ine ndine m'bale wanu. Tsopano, izo zingamuthamangitse munthu aliyense kuchoka pa ntchito. Izo zikanamupangitsa aliyense amene amakonda Khristu kuthawa ku chinthu chomwecho.

<sup>31</sup> Ine ndinapita kwa Ambuye kuno osati kale kwambiri, pamene ine ndinamva izo koyamba, pafupifupi chaka chapitacho. Ndiyeno ine ndinapita kwa Ambuye ndipo Iye anandilozera ine ku Lemba kuti pamene Yohane anabwera uko akulalikira, kuti iwo anali asanakhale naye mneneri pa dziko lapansi kwa zaka zochulukira, mpaka izo zikanati...iwo anazizwa onse mmitima mwawo, akuganiza kuti mwina Yohane anali Mesiya. Kotero ndiye ine...Yohane, iwo anapita nakamufunsa iye, ndipo iye anati iye sianali. Inu mumaziwerenga izo mu Luka mutu wa 3, ndime ya 15. Ndipo kotero ndiye...Koma izo zinakhala ngati zachita bata, kotero ine ndinazisiya izo zipite monga choncho.

<sup>32</sup> Koma ndiye pamene izo zinafika ku izi, ndiye ine ndinadziwa kuti chinachake chikuyenera kuti chichitidwe. Ndipo ine ndikunena izi, “Kuti masomphenya ndi Mngelo wa Ambuye amene anawonekera pa mtsinje,” (ngati uwu ungakhale uthenga wanga wotsiriza kapena chinthu chotsiriza kwa mpingo, ku dziko) “zinthu zimenezo ndi Choonadi, monga momwe Mngelo wa Ambuye.”

<sup>33</sup> Ndipo ine ndinkayima njii ngati anthu ankanditchula ine mneneri nthawi zambiri, chifukwa *mneneri* mu chipangano cha Chingerezi ndi basi “mlaliki, wonenera, wolosera Mawu,” ndi zina zotero. Ine ndingayime pa chimenecho chifukwa inu mukhoza kukhala ngati mukukankhira izo pansu; koma zikafika ponditcha “Khristu Wodzozedwa,” kapena chinachake, izo zinali zondikulira. Kotero ine sindikanatha kuzipirira nazo.

<sup>34</sup> Ndipo kotero ndiye zokhudza...ine ndabwera... Nditachoka ku msonkhano ku Canada, Ine ndinapeza kuti njira imeneyo uko mu Eskimos kapena Amwenye kumtunda uko, izo zinali zitafika pakati pawo.

<sup>35</sup> Ndipo kotero izo zinangonding'amba ine yense. Ndipo ulendo wokasaka umene ndinawukonza kalekale, ine sindinathe kukhala nawo iwo. Ine ndinkaopa ngozi ya kokasaka, ngati inu mukumvetsa zomwe ine ndikutanthauza. Ine ndinali wonjenjemera kwambiri, moyipirapo kuposa momwe ndayimira pano tsopano. Ndipo ine sindikanakhoza basi kuzipirira izo

kenanso, kuganiza kuti zaka sarte wani za utumiki zinapita pansu pa ngalande ya mdierokezi, kulowa mu... Pamene ine ndapita, kodi iwo adzanena chiyani? “Apo iye ali, ndicho ndendende chimene chinali”; ndi kukopa konse komwe ine ndinali nako pa anthu, ndiye inu mukuwona pamene izo zikanakhala, ine ndikanakhala wotsutsakhristu. Ndipo ine sindikanatha kuzipirira izo!

<sup>36</sup> Ine ndinaganiza, “Ine kulibwino ndifere kuno mu nkhalango, monga ine nditagwera pa mfuti yanga kapena chinachake, kusiyana...” Ndipo ine ndinawona ndinali... Ndiye ine ndinaganiza za Joseph wanga wamw’ono, ndi ena otero, amene ankayenera kuti aleredwe. Ndipo ine ndinalibe chikhaliwe choti ndikanasaka, kotero ine ndinangochoka ku nkhalango ndi kubwera kunyumba.

<sup>37</sup> Ndipo ine ndakhala wong’ambidwa pafupifupi masiku eyiti kapena teni, mu njakata kotero kuti ine—ine ndinkaganiza kuti ndimasokonezeka malingaliro. Ndipo ine ndinangomupempha aliyense kuti akhale kutali ndi ine ndi kundisiya ndekha chifukwa ndiri mu njakata yotero ndi wamanjenje ndi wokhumudwa ndi wosweka yense mzidutsa.

<sup>38</sup> Ndipo ine ndinadabwa; ngati iye akanakhala mdani wanga wina, izo zikanakhala zabwino, koma ine ndikanangoseka pa izo ndi kumapitirira; koma pamene zinafika pokhala abale ofunika, alongo ofunika, ndiye ndi zomwe zinandipweteka ine. Ndipo ine ndinati, “Ambuye, wamkulu... chinthucho chandikulira ine, ine ndikuyenera kungotuluka ndi kungochisiya mmanja Mwanu. Ine—ine sindikudziwa china choti ndichite.”

<sup>39</sup> Mausiku angapo apitawo, kuti nditsimikizire izo, ndinali ndi—kuchezeredwa kwa Ambuye. Ndipo ndinawona a mtengo wapatali akulera a—njoka, yomwe inali yachikasu ndi yakuda, ndipo akumandiuza ine, cha pamene, ndipo icho, ndipo chinthucho chinandikantha ine pa mwendo. Koma magaziwo anali olemera kwambiri kotero sizinagwire ntchito pa ine. Ndipo ine ndinayang’ana pansu, ndipo apo ndi pamene ine ndinali nditalumidwa kale m’mbuyomu. Ndipo ine ndinatembenuka mwachangu ndi mfuti ndi kuwombera a—chinthucho, ndipo icho chinamenya pakati pomwe pa chinthucho.

<sup>40</sup> Ndipo m’bale anati... Ine ndinatembenuka ndi mfuti yanga kuti ndiwombere mutu wake, ndipo iye anati, “Musachite zimenezo, ingotengani ndodo yomwe ili pamene pafupi nanu.” Ndipo pamene ine ndinatembenuza nsana wanga kuti ndinyamule ndodoyo, iyo inadziguwetsera m’madzi ena, chithaphwi chaching’ono chabe cha madzi.

<sup>41</sup> Ndinati, “Chabwino, izo sizinapwetete motalika kwambiri tsopano chifukwa ine ndikukhulupirira m’baleyo akuzindikira (abalewo) izo zimene zikanadzachitika.” Ine ndinati, “Itero... Iyo yavulazidwa kwambiri, kotero iyo ifa.”

<sup>42</sup> Ndipo ine ndikuwafunsa ambiri a mamembala anga a mpingo wanga kuno, mu kachisi uyu ndi M'bale Neville ndi ine, amene abwera kundifikira ine ndi funso lomwelo: Abale, alongo, kodi ine sindinayesetse kukhala mtumiki weniweni wa Khristu pamaso panu? Kodi sindinayesetse kukhala m'bale wanu? Tsopano, kulikonse kumene kuli, ndi mzimu pa anthu ofunika. Anthu ambiri andifunsapo ine zimenezo. Koma ndi—ndi mzimu, koma ndikuyembekeza kuti lero ulandira bala lakupha ndipo udzafa msanga kuti ine ndibwerenso ku utumiki. Mpaka pamenepo, ine ndikufunsani inu aliyense, mundipempherere ine. Ine sindikudziwa chomwe ndingachite. Malo anga akugulitsidwa. Ine sindingathe kupirira nazo, ine—ine—ine ndikakhala pano, ine ndikhala wamisala kwathunthu. Ndipo ine. . . Ine ndikukupemphani inu kuti mundipempherere ine.

<sup>43</sup> Ndipo, kumbukirani, ngati inu munayamba mwandikhulupirirapo ine, ngati inu munayamba mwandikhulupirirapo ine kuti ndine wantchito wa Khristu, kumbukirani, “Kumeneko ndi kulakwa! Ndi zabodza!” PAKUTI ATERO AMBUYE! “Ndi zolakwika! Musakhale ndi chochita ndi izo!” Ine ndine m'bale wanu.

Tiyeni tiweramitse mitu yathu:

<sup>44</sup> Atate a Kumwamba, thupi langa likunjenjemera, manja anga akufinyika pamodzi, zala zanga zakokeka mu nsapato zanga. O Mulungu, khalani wachifundo. Kodi ine ndinayamba ndachitapo chiyani, Ambuye, kuti ndiyenere izi? Ine ndikupemphera kuti Inu mukhale wachifundo kwambiri kwa ine, Ambuye, ndi kwa onse. Ndi kumtunda uko, ndi anthu ofunika okondeka awo, mulole iwo awone cholakwitsa chawo ndi chimene iwo achita, Ambuye, kuswa mtima wa m'bale wawo ndi kuti. . . osati m'bale yekha, komanso Mpulumutsi wathu, Atate wathu wa Kumwamba. Ine ndikupemphera kuti Inu mutikhululukire ife zolakwitsa zathu, Ambuye. Mulole Magazi oyera a Khristu tsopano akokere umunthu wathu pamodzi, Ambuye, ndipo chodala chikhale Chimango chomwe chimamanga mitima yathu mu chikondi Chachikhristu ndi chiyanjano.

<sup>45</sup> Mulungu, mulole mdani amene anawafikira abale athu ndi alongo athu. . . alandire bala lakupha kuti asakhaleponso mopitirira; mulole izo zingofa, Ambuye. Inu mukachita izo, Atate, ine ndidzabwereranso ku ntchito kachiwiri. Koma mpaka pamenepo, Ambuye, ndine wantchito wanu wosweka mtima, wodikira, woyembekezera. Ndi zoposa chirichonse chimene ndingathe kuchita. Ndi misozi ndi kulira ndi kukopa ndinayesera, Ambuye, molimba (Inu mukuwudziwa mtima wanga.) kuziyimitsa izo zisanafike patali, koma izo zinapita mopitirira chirichonse chomwe ndikanachita. Kotero, Atate, ine ndikuzipereka izo mmanja Mwanu kuchokera pa guwa



lino kupita kumene ine ndalalikira kwa zaka zonsezi. Ine ndikuzipereka izo mu Dzanja Lanu.

<sup>46</sup> Tsopano, Inu musamalira izo, Atate, mwa njira Yanu Yomwe Yauzimu. Ndipo pamene izo zonse zatsirizika ndipo chirichonse chatha, ndiye wantchito Wanu adzabwerera. Mpaka pamenepo ine ndikhala ndikuyembekezera kumva kuchokera kwa Inu, Ambuye.

<sup>47</sup> Tidalitseni ife tsopano ndipo tipatseni ife utumiki waukulu lero; pamene ife tiri pano osati palimodzi chifukwa cha izi, koma kuti tingozipanga izo momveka, poyera, pamaso pa dziko. Kuti iwo akhoze kudziwa, Atate, kuti ine ndimakukondani Inu ndi kukukhulupirirani Inu ndipo ndakuyimirani Inu, ndipo—ndipo ndikufuna kuteru, Ngati ine ndikuyenera kuti ndipite, ndiloleni ine ndipite, Ambuye, ndi mtima woyera ndi mbiri yeniyeni kuti ine ndinakukhulupirirani Inu ndi kukudalirani Inu. Perekani izi. Ndipo ine ndidzakutamandani Inu ndipo ife tidzakupatsani Inu ulemmerero kupyola mu mibadwo yonse imene ikudza kudzera mwa Yesu Khristu. Amen.

<sup>48</sup> Tsopano, mu Malemba, tiyeni ife titembenzire mu Baibulo ku. . . Ndimaganiza mmawa uno chikhala chinthu chabwino, ngati M'bale Neville sasamala, kuti tingopitirira kwa maminiti pang'ono mu. . .

<sup>49</sup> Tsopano, ine. . . Musandilole kuti ndimvenso zikutchulidwanso kamodzi pakati panu. Ingopempherani ndi kuchitsekereza icho, chitsekerezeni icho. Mukuona? Ine sinditero. . . Ine—ndiri—ndiri ndi zaka fifite thuu zakubadwa, koma ine ndikuganiza mwinamwake, ngati Mulungu angandisunge ine, ndatsala ndi moyo pang'ono, ndipo ine ndikufuna kuti ndigwiritse ntchito gawo lililonse la nthawi yanga kwa Khristu. Koteru, kumbukirani, ndikuchoka chifukwa ndikukakamizika kuti ndichite izo.

<sup>50</sup> Tsopano, mu Bukhu la Chibvumbulutso, mu mutu wa 4 pamene ife tinalekezera tsiku lina pamene ife tinali mu phunziro. . . Chibvumbulutso, mutu wa 4, ine ndikukhulupirira, pa gawo lotsiriza la ndime, la mutuwo. Chabwino, ndi angati amakonda Chibvumbulutso? Zodabwitsa! Tsopano, ine ndikukhulupirira ife tinasiyira pa wa 5—mutu wa 5, sichoncho ife? Ife tinasiyira, mutu wa 4, Zorengedwa zamoyo zinayi. Tsopano, tiyeni tiyandikire Mawu tsopano, kuyiwala kuti zinthu zimenezo zinali zakale.

<sup>51</sup> Atate Mulungu, Inu mutithandize ife tsopano pamene ife tiri amanjenje, koma ife tikuyandikira Mawu. Kuyiwala zomwe zinali kale, ife tikulimbanira tsopano ku chizindikiro cha mayitanidwe apamwamba, mayitanidwe apamwamba a utumiki kukhala wantchito wa Khristu. Tipatseni ife Mawu mmawa uno ndi kudyetza miyoyo yathu yanjala, pakuti ife tikukhumba, Ambuye, ndi kuyembekezera kudzoza kwa mtengo wapatali

uko kwa Mzimu Woyera. Bwerani pakati pathu, Ambuye, kutikhululukira machimo athu ndi zolakwa zathu ndi kutilola ife kukhala antchito Anu. Pakuti ife tikupempha izi mu Dzina la Yesu. Amen.

<sup>52</sup> Tsopano, ife tinatenga mibadwo ya mpingo, Mibadwo Seveni yotsiriza ya Mpingo. Ndiyeno, tsopano, ine ndikukhulupirira ena a iwo akuyesera kuti . . . azilemba izi, mibadwo ya mpingo. Ndiye ife tinabwera mu mutu wa 4 wa Bukhu la *Chibvumbulutso Cha . . .* Ichi ndi chiyani? *Chibvumbulutso Cha Yesu Khristu. Chivumbulutso*, chotchedwa mu Chilatini, *Apocalypse*, chimene chimatanthauza “kuwululidwa, kuchotsa a—chivindikiro cha, kuwonetsa, kuyika poyera,” kubweretsa vumbulutso la Yesu Khristu yemwe Anali, Ali, ndipo Adzabwera Mtsogolo, Muzu ndi Mphukira ya Davide.

<sup>53</sup> Tsopano, mu mutu wa 4, ife tikupeza kuti Yohane anakwatulidwira Kumwamba atatha kuwona mibadwo ya mpingo. Ndikungotenga maziko pang’ono tsopano, ndipo kenako tidzatero . . .

<sup>54</sup> Mwinamwake zingakhale zabwino kuti tiwerenge ndime zingapo za mutu wa 5, ndipo kenako tiyambira pomwepo ndi maziko.

*Ndipo ndinawona m’dzanja lamanja la Iye wakukhala pa mpandowachifumu bukhu lolembedwa mkati ndi . . . kumbuyo, losindikizidwa ndi zisindikizo zisanu ndi ziwiri.*

*Ndipo ndinawona mngelo wamphamvu wakulalikira ndi liwu lofuula, Ndani ali woyenera kutsegula bukhulo, ndi kumasula zisindikizo pamenepo?*

*Ndipo panalibe munthu kumwamba, kapena pa dziko lapansi, kapena panso pa nthaka, anali wokhoza kutsegula bukulo, ngakhale kuyang’ana pa ilo.*

*Ndipo ndinalira . . . chifukwa panalibe munthu anapezeka woyenera kutsegula ndi . . . kuwerenga bukhulo, ngakhale kuyang’ana pa ilo.*

*Ndipo m’modzi wa akulu anati kwa ine, Usalire: tawona, Mkango wa fuko la . . . la Yuda, Muzu wa Davide, wapambana kutsegula bukhulo, ndi kumasula zisindikizo zisanu ndi ziwiri.*

*Ndipo ndinawona, ndipo, taonani, pakati pa mpandowachifumu ndi . . . zirombo zinayi, ndi pakati pa akulu, panayima Mwanawankhosa ngati iye anali ataphedwa, wokhala nazo nyanga seveni ndi maso seveni, yomwe ili Mizimu seveni ya Mulungu yotumizidwa ku dziko lonse lapansi.*

*Ndipo iye anadza natenga bukhulo kuchokera mu dzanja lamanja la iye amene anakhala pa mpandowachifumu.*

Ndizo ndime seveni zoyamba.

<sup>55</sup> Tsopano, tsopano, mu mutu wa 3 wa Chibvumbulutso, ife tikupeza kutha kwa M’badwo wa Mpingo, zomwe zinathera ndi Laodikaya, m’badwo wa mpingo wofunda. Ndiye ife tikupeza kuti, mwamsanga zitatha izo, Yohane anatengeredwa mu Mzimu, kupita uko Kumwamba. Ndipo iye anawona zinthu zimene zinali, ndi zimene zinali nkudza, ndi zinthu zimene zinalipo. Tsopano, ife tikupeza, mpingo sukuwonekeranso mpaka mutu wa 19 wa Chibvumbulutso, ndiyeno iye akubwerera pamodzi ndi Mbuye wake, wotsukidwa mwaulemerero ndi Magazi.

<sup>56</sup> Tsopano, mu chobwereza chotsiriza ichi, kwa maziko aang’ono kuti tikhazikike pamene Yohane ali tsopano, ife tinazipeza izo mu uthenga wotsiriza. . . Ine ndimangoyang’ana pa iwo mwachidule dzulo, zina mwa nkhani zomwe ndinazinena. Ndipo Yohane anyamulidwa kupita Kumwamba ndipo anawona zinthu zimenezo. Ndipo ine ndinali nditazindikira mmenemo kuti Iye anali atandipatsa ine vumbulutso, kuti. . . Inu mukudziwa, pambuyo pa chiwukitsiro Chake ambiri anali ndi Iye, ndipo ena anati, “Kodi chidzachitike nchiyani kwa mwamuna uyu yemwe akutsamira pa chifuwa Chanu (Yohane)?”

<sup>57</sup> Yesu anatembenuka ndipo anati, “Ziri ndi chiyani kwa inu ngati iye akhalabe kufikira Ine nditadza?” Koteri Iye sanatero. . .

<sup>58</sup> Ndiye apo panatuluka chiphunzitso. Mukuwona momwe zingayambire mophweka? Apo panatuluka chiphunzitso kuti—kuti “Yohane sadzafa mpaka iye atamuwona Yesu akubwera, kapena mpaka Kudza Kwachiwiri.” Baibulo linati panali chiphunzitso chinatuluka cha zimenezo.

<sup>59</sup> Komabe, Yesu sananene konse izo mwanjira imeneyo. Iye anati, “Kuli chiyani kwa inu ngati iye akhalabe kufikira Ine nditadza?”

<sup>60</sup> Tsopano, ife tikupeza kuti iye anyamulidwa kupita kumwamba ndipo anawona kuchokera pamenepo mpaka kudza kwa Ambuye, ngati kuti iye anali pamenepo ndipo anaziwona zonse zikuchitika. Yohane iyemwini sanakhale moyo. . . Iye anakhala moyo zaka nainte chakuti, ndipo kenako anafa mu a—imfa yachibadwa (mmodzi yekhayo wa atumwi) atatuluka mu ukapolo kuchokera pa chisumbu cha Patmo.

<sup>61</sup> Tsopano, pali mfundo imodzi yodziwika bwino yomwe ndingafune. . . (Ine ndikuganiza iwo ayitsitsa. . . bolodi yanga pansu, koma. . .) Ine ndikufuna kuti nditsindike pa izo pang’ono ife tisanakhudze chinthu chofunikira ichi. Oh, izi ndi zaulemerero! Wodabwitsa, mutu wodabwitsa.

<sup>62</sup> Ndiyeno mutu wotsatira womwewo ukuyamba ndi kutsegula zisindikizo izi. Oh, mai! Ndiyeno ife tiyenera kuti tidumphe kuchokera pamenepo ndi kupita ku malo osiyanasiyana mu Baibulo, kuti titenge zisindikizo izi pamene zikutsegulidwa ndi zomwe zinsinsi za izo ziri. Oh, izo ndi zaulemerero, zolemera basi ndi mavitamini auzimu!

<sup>63</sup> Tsopano, ife tikuwona kuti chimodzi mwa zinthu zapamwamba kwambiri zomwe ine ndikufuna kuti ndikope tcheru chanu, zinali Zorengedwa zamoyo (za gawo lotsiriza la mutu wa 4) zimene Yohane anaziwona zikuyang'ana Likasa la Pangano. Inu mukukumbukira momwe iwo anakhazikika monga Israeli mu kuguba kwake? Iwo anali nayo, tsopano, pamenepo, inali nkhope ya Chorengedwa chamoyo. Ndipo ife tinapeza kuti Zorengedwa izi sizinali Angelo, ngakhalenso iwo sianali anthu. Iwo anali Akerubi. Ndipo ife tinazipeza izo mu Chipangano Chakale ndi likasa. Ife timazipeza mu Chipangano Chatsopano. Ndiyeno ife tikuwapeza iwo mu Kudza kwa Ambuye kachiwiri, Akerubi akulondera mpando wachifundo.

<sup>64</sup> Mpando wachifundo umene palibe munthu akanawuyandikira pokhapokha ngati panali chitetezero kwa munthu ameneyo, njira yokhayo imene malo opatulika... Pamene iwo unkawazidwa magazi, ndiye iwo unadzakhala mpando wachifundo. Koma magazi atachotsedwa, ndiye iwo unadzakhala mpando wachiweruzo.

<sup>65</sup> Ndipo, oh, mai, palibe mmodzi angayime pa ziweruzo za Mulungu. Chinthu chokhacho chimene ife tingachifunefune ndi chifundo, osati chiweruzo, osati chilunga-... chilungamo. Ife sitingathe kuchifikira chilungamo Chake; chifukwa, chilungamo Chake, Iye adzayenera kusunga Mawu Ake; ndipo kusunga Mawu Ake, "Tsiku limene mudzadya za umenewo, tsiku limenelo inu mudzafa." Ndani angafune chilungamo? Ine sindikufuna chilungamo. Ine ndikuyitanira chifundo. Mai, kulola chifundo cha Mulungu... Ndipo mpando wachifundo unawazidwa!

<sup>66</sup> Koma panali nthawi ya kuyeretsa kwa malo opatulika, pamene iwo unali mpando wachiweruzo utali wonse pamene magazi anali atachoka pa mpandowo.

<sup>67</sup> Tsopano, ife tikuyandikira nthawi imeneyo *tsopano*. Ife tsopano tikuyandikira, mu m'badwo uno, kuyeretsedwa kwa malo opatulika ndi ziweruzo zikubwera pa dziko lapansi. Mukuona? Bola ngati Magazi ali pamenepo, Mulungu sangakhoze kuwononga dziko lapansi; bola ngati Magazi ali pamenepo, palibe amene ali wochimwa pamaso pa Mulungu. Aliyense ndi wolondola, chifukwa pali Chitetezero cha aliyense. Koma ngati inu mulephera kuvomereza Chitetezero chimenecho ndi kupita mu Kukhalapo Kwake, ndiye ndinu wochimwa, inu mwapitirira chifundo chimenecho. Ndiye inu mwadziweruza nokha. Koma tsopano pamene pali chifundo...

Koma kukadzafika kuyeretsa kwa malo opatulika, Magazi adzachoka pa mpando wachifundo ndipo kenako mkwiyo wa Mulungu udzagwera pa dziko lapansi. Oh, mai! Mulungu atichitire ife chifundo, kuti ife tisakapezeke mu tsiku limenelo opanda chifundo cha Mulungu.

<sup>68</sup> Tsopano, ife tikuwona mmenemo . . . Ndiyesera kuti ndikhale ngati ndikuzipanga zauzimu apa, kapena kukujambulirani izo ndi manja anga, kuti panali ngodya foro momwe Israyeli anamangira misasa. Iwo anayika—likasa pakati, ndipo pa mbali zinayi za chihema panali mafuko atatu a Israeli, ndipo mafuro atatu ndi thwelovu, kapena ma firii anayi, kani, thwelovu. Ndipo atatu aliwone anali ndi mutu. Ndipo mutu uliwonse wa fuko . . .

<sup>69</sup> Mmodzi wa iwo anali Rubeni, ndipo iye ankamanga msasa nthawi zonse—kummwera. Iye anali mutu wa munthu. Ndipo Efraimu anali kumadzulo, ndi mafuko atatu, iye anali—ng’ombe. Ke . . . Kenako kummawa kunali Yuda, amene ali mkango. Ndipo kumpoto kunali Dani, amene anali mphungu. Tsopano, zindikirani. Inu mukuwakumbukira iwo? Nonse a inu mukukumbukira bwino, momwe ife tinazijambulira izo: mphungu, ndi ng’ombe, ndi mu—munthu, ndi mkango.

<sup>70</sup> Tsopano, inu mukuzindikira, Yuda amalondera chipata chakummawa. Ndipo Khristu ndi “Mkango wa fuko la Yuda.” Iye adzatsika kuchokera ku thambo la kummawa nkulowera mwa njira ya pa chipata. Iye amachokera ku chipata cha kummawa kuchokera ku fuko la Yuda. Ndipo Iye “Mkango wa fuko la Yuda.”

<sup>71</sup> Ndipo ife tikupeza, mu uthenga wathu ukubwera mmawa uno, kuti Iye akadali kulengezedwa “Mkango wa fuko la Yuda, Muzu, chiyambi chomwe cha Davide.” Davide anali mfumu, Kwamuyaya. Ndipo Khristu akukhala pa mpandowachifumu wa Davide mu Zakachikwi, amene ali Mfumu Yamuyaya. “Sipadzakhalanso mmodzi womulaka Davide.” Aleluya! “Sipadzakhalanso mmodzi womulaka Davide!” Mulungu analonjeza zimenezo, anati, “Palibe amene akanamulaka Davide, ngakhale mmodzi.”

<sup>72</sup> Inu mukuti, “Nanga bwanji lero, oweruza Achiyuda amenewo ali kuti?”

<sup>73</sup> Iye akadali nayo Mbewuyo, Kristu ndi Mwana wake monga mwa thupi. Apo mmodzi wakhala pamenepo. “Davide sadzalephera.” Uko nkulondola. Ndipo Khristu ndi “Mkango wa fuko la Yuda” umenewo kumene Davide anatulukirako.

<sup>74</sup> Tsopano, ife tikupeza kuti iwo anali alonda ku mpando wachifundo. Iwo ankayang’ana mpando wachifundo. Palibe chinabwera kwa icho, chinawoloka mafuko choyamba icho chisanafike ku mpando wachifundo. Munthu aliyense wofuna kupereka moyo wake, m’Israeli aliyense amene ali mu msasa akanafa chirichonse chisanalowe mu msasa umenewo ndi

kutenga mpando wachifundo umenewo. Ndipo tsopano ife tikupeza kuti ilo linali dongosolo la Chipangano Chakale.

<sup>75</sup> Ndipo mu dongosolo la Chipangano Chatsopano ife tikupeza chinthu chomwecho, kuti iwo unkalonderedwa, mpando wachifundo. Oh, ine ndikuyembekeza inu mukumvetsa izo! Mpando wachifundo ukadali kulonderedwa, ukadali nawo alonda. Tinapeza kuti alonda amenewo ndi Mateyu, Marko, Luka, ndi Yohane, akulondera Bukhu la Machitidwe, machitidwe a Mzimu Woyera ochitidwa pakati pa atumwi, lomwe liri—Bukhu la Machitidwe la Chatsopano la Chipangano Chatsopano. Ndipo alembi foro a Mauthenga, Mateyu, Marko, Luka, ndi Yohane, onse amalondera mpando wachifundo umenewo kusonyeza kuti ndi Mulungu, Mzimu Woyera lero. Lemba lirilonse, Mateyu, Marko, Luka, ndi Yohane, aliyense wa iwo adzayikira kumbuyo Uthenga woona wa Ambuye Yesu Khristu ndi machitidwe za Mzimu Woyera.

<sup>76</sup> Tsopano, pamene ife tipyola Izo ndiye umenewo si Iwo. Koma Iwo umayikira kumbuyo Uthenga woona! Monga ife tikuzipezera mu Machitidwe 2:38, kumene, “Lapani, ndi kubatizidwa mu Dzina la Yesu Khristu kuloza ku chikhululukiro cha machimo anu.”

<sup>77</sup> Ndipo lero iwo atenga Dzina la “Atate, Mwana, ndi Mzimu Woyera” kuti abatizidwe mo. Palibe Lemba la izo! Palibe maziko. Panalibe—panalibe kanthu koti kalondere zimenezo, panalibe kanthu! Inu mukuti, “Mateyu ananena zimenezo.” Mateyu ankawulondera Iwo. Mateyu 28 . . . 1:18 akuti:

*. . . kubadwa kwa Yesu Khristu kunali motere: Pamene . . . amayi ake Mariya anatomeredwa ndi Yosefe, iwo asanabwere pamodzi, iye anapezeka ndi mwana wa Mzimu Woyera.*

*Zonsezi zinachitika pamene . . . Yosefe mwamuna wake, (kani) pokhala munthu wolungama, . . . osati mwadala kuti amunyazitse iye poyera, anaganiza kuti—kuti amusiye iye mwamseri, motere.*

*Koma posinkhasinkha iye zinthu izi, taonani, mngelo wa Ambuye anawonekera kwa iye mu loto, akuti, Yosefe, iwe mwana wa Davide, usawope kudzitengera wekha Mariya mkazi wako: pakuti icho cholandiridwa mwa iye chiri cha Mzimu Woyera.*

<sup>78</sup> Ndiye, Mzimu Woyera ndi Mulungu Atate ali Munthu yemweyo kapena Iye anali ndi atate awiri. Mukuona? Koteru inu mukuona!

*Ndipo iye adzabala mwana, . . . adzamutcha dzina lake YESU: . . .*

*. . . ndipo ichi chinachitika, kuti zikakwaniritsidwe . . . zonedwa . . . mneneri, . . .*

<sup>79</sup> Mulungu adzakhala ndi ife, wotchedwa Emanuela, amene ali Mulungu, Atate, Mwana, ndi Mzimu Woyera, mu Dzina limodzi (Yesu Khristu) amene amalondera chipata chimenecho motsutsa cholakwika.

<sup>80</sup> Masiku angapo apitawo mu Chicago, pamaso pa bungwe la atumiki aku Chicago, Chicago wamkulu. . . Ine ndinadziwa. . . Mzimu Woyera unandidzutsa usiku ndi kundiuza ine, “Ima pa zenera.” Anati, “Pali gulu la atumiki ndipo akukukonzera iwe kadzutsa.” Anati, “Usamale, iwo akuwukira iwe pa izi.”

<sup>81</sup> Ine ndinati, “Zikomo Inu, Ambuye.” Iye anandiwonetsa ine pamene izo zikanati zidzakhale.

<sup>82</sup> Ndipo ine ndinapita ndi kukawauza atumiki ena, M’bale Carlson ndi M’bale Tommy Hicks, momwe izo zikanati zidzakhali. Ine ndinati, “Malo omwe inu munakonzza, izo sizikakhala choncho. Ife tikakhala mu malo ena.” Anandiuza momwe Dokotala Mead akakhali; momwe munthu wachikuda akabweremo, nakhala *chonchi*; ndi zonse za izo.

<sup>83</sup> Ndiye mmawa umenewo, ndipo iwo anati. . . Mwana wanga anandiuza ine, iye anati, “Adadi, inu mukupita kumeneko mumkangano umenewo?”

<sup>84</sup> Ndipo ine ndinati, “Ine sindikupita kuti tikakangane. Ine ndikupita kumeneko, wodzozedwa ndi Mzimu Woyera, ndi Mawu a Mulungu amene akalondere mpando wachifundo umenewo, bola ngati Iye ali pamenepo.”

<sup>85</sup> Kotero pamene ife tinafika kumeneko, iwo asanakhale nkomwe ndi mwayi wofunsa chinthu chimodzi, Mzimu Woyera unayankhula kwa ine, unati, “Tsopano ndi nthawi yoti unene izo.”

<sup>86</sup> Ine ndinati, “Ine ndikudziwa chifukwa chomwe inu muli pano.” Ndipo ine ndinati, “Tsopano, M’bale Hicks, ndi inu ndi M’bale Carlson, mtsogoleri wa Christian Businessmen,” ine ndinati, “kodi zonse siziri ndendende basi momwe Mzimu Woyera unandiuza ine dzulo? Kuti inu simunapeze chipinda chimenecho, ife tikanati tidzakhale kuno?” Ndipo iwo anangochipeza icho mmawa umenewo. Ndipo ine ndinati, “Tsopano penyani, aliyense anayikidwa basi momwe Iwo unanenera kufi izo zikanadzakhala.” Ine ndinati, “Chinthu chimene mukufuna kuti mundifikire nacho ine ndi pa Dzina la Yesu Khristu kwa ubatizo.”

<sup>87</sup> Ndipo pamene ife. . . Mzimu Woyera unayamba kutenga Mawu a Mulungu ndi kuwawulula Iwo ndi kuwatanthauzira Iwo pansi monga choncho, pamene gulu lonse lija la atumiki a utatu atakhala pamenepo, akufika pansi pa tebulo ndi kugwirana chanza wina ndi mzake ndipo misozi ikuyenderera mmasaya mwawo. Ndipo ine ndinamvetsedwa kuti sevente thuu a iwo akubwera kuno ku kachisi uyu kuti ine ndiwabatize iwo mu Dzina la Yesu Khristu.

<sup>88</sup> Mpando wachifundo ukulonderedwa, mwaona, Mzimu Woyera ukulondera mpando wachifundo. Ife tiyenera kuzisunga izo ndendende basi... Kuwalola Mawu a Mulungu awo... amithenga aakulu awo atakhala pamenepo, Mateyu, Marko, Luka, ndi Yohane, amene amayikira kumbuyo machitidwe aliwonse a Chipangano Chatspano icho.

<sup>89</sup> Ndipo tsopano, tsopano, ndizo ndendende zomwe ine ndinanena mu gawo loyamba la uthenga wa mmawa uno, tiyeni tizisunge izo pamenepo motetezedwa ndi Uthenga. Kodi inu mukuona? Mukuona? Zisungeni izo apo pomwe Mauthenga azidzaulondera Iwo.

<sup>90</sup> Tsopano, ife tikupeza mmenemo, iwo ankalondera mpando wachifundo wa Mulungu mu Chipangano Chakale; ndipo pamenepo, Mateyu, Marko, Luka, Yohane, onse a iwo. Ndipo ngakhale Mkango wa fuko la Yuda unapereka moyo Wake kuti ulondere mpando wachifundo umenewo, kuwulola iwo ukonkhedwe ndi Magazi Ake Omwe. Ndipo apo Iye wayima mmawa uno, lero, Mgonjetsi wamkulu amene adzatsika kuchokera Kummawa tsiku lina ndipo ife tidzamuwona Iye.

<sup>91</sup> Tsopano, ife tikutembenezira mwamsanga, chifukwa ine ndikudziwa kuti pali utumiki wa ubatizo. Kodi Bukhu la zisindikizo seveni ili ndi chiyani? Oh, ndi chinthu chachikulu bwanji! Kodi munazindikira momwe akunenera apa, “Zinali zisindikizo seveni *kumbuyo* kwa Bukhulo”? Ndi chinachake... Oh, Mulungu atithandize ife tsopano ndi kutipatsa ife kulimbika mtima, ndipo mwinamwake posakhalitsa ine ndikhoza kuzifikitsa izo kwa inu. Penyani, izi sizinalembedwe mu Mawu, izo zasindikizidwa kumbuyo kwa Mawu. Bukhulo linasindikizidwa ndi zisindikizo seveni izi. Chinsinsi chonse cha Bukhulo chasindikizidwa mu zisindikizo seveni izi. Uwu ndi umodzi mwa mitu yayikulu kwambiri mu Bukhu lonse la Chivumbulutso. Penyani:

*Ndipo ine ndinawona mu dzanja lamanja la Iye wakukhala pa mpandowachifumu bukhu lolembedwa mkati ndi... lolembedwa mkati (Mkati ndi molembedwa, ndi zomwe ife tikuwerenga mmawa uno.) ndi... kumbuyo kwake, losindikizidwa ndi zisindikizo zisanu ndi ziwiri.*

Kunja kwa Baibulo, chimene Baibulo silimanena nkomwe, izo zasindikizidwa mkati umu ndi zisindikizo seveni: zinsinsi za Mulungu.

<sup>92</sup> Tsopano, ndi chiyani icho? Tsopano, zindikirani. Chisindikizo chimayimira katundu womalizika, chinachake chomwe chayesedwa kale, kutsimikiziridwa, ndiyeno nkusindikizidwa. Ali kuti... Tiri ndi chikole cha chipulumutso chathu tsopano pa kusindikizidwa ndi Mzimu Woyera. Ndicho chikole cha chipulumutso chathu.



93 Tiyeni tibwerere mmbuyo miniti yokha. Ine—ine ndiri nalo Lemba lolembedwa apa, angapo a iwo, ine ndiribe . . . sindikhala ndi nthawi yoti ndipite kwa onse. Koma tiyeni tibwerere ku Aefeso, mphindi yokha, ndi kuweringa . . . mu mutu 1 wa Aefeso, kotero kuti inu mukhoze kupeza tanthauzo lenileni.

*Paulo, mtumwi wa Yesu Khristu mwa chifuniro cha Mulungu, kwa oyera mtima amene ali ku Efeso, . . .*

94 Ndipo, kumbukirani, Yohane anali ndi kalata iyi yopita kwa Aefeso, ku Efeso ndi okhulupirika mwa Khristu, iwo amene Paulo anawalalikirira ndi kuwakuza, kuwalera ndi Uthenga. Mukuona?

*. . . Efeso, ndi kwa okhulupirika mwa Khristu . . .*

95 Ndiwo omwe ali kale mwa Khristu. Kodi ife timalowa bwanji mwa Khristu? “Mwa Mzimu umodzi ife tonse timabatizidwa kulowa mu Thupi limodzi,” lomwe liri Thupi la Khristu.

*Chisomo chikhale pa inu, ndi mtendere, zochokera kwa Mulungu Atate wathu, ndi . . . Ambuye Yesu Khristu.*

*Wodala akhale Mulungu ndi Atate wa Ambuye wathu Yesu Khristu, yemwe watidalitsa ife ndi madalitso onse auzimu mu malo amwambamwamba mwa Khristu Yesu:*

96 Taganizani za izo tsopano! Iye watidalitsa ife ndi chisomo chonse chakumwamba, madalitso, pamene ife tisonkhana pamodzi mwa Khristu Yesu (monga okhulupirira, Mpingo wosankhidwa, woyitanidwa, woyikidwa pambali). Iye watisindikizira ife mkati ndi Mzimu Wake Woyera, ndipo tsopano akuwulula kwa ife zinthu zonse zimene ziri mtsogolo kwa ife. Tsopano ife tikufika ku zisindikizo seveni.

*Molingana monga iye anatisankha ife mwa iye asanakhazikitsidwe maziko a dziko, kuti ife tikhale oyera ndi opanda chilema . . . mu chikondi:*

*Atatikonzeratu ife ku kukhazikitsidwa kwa ana mwa Yesu Khristu kwa Iyemwini, monga mwa kukondweretsedwa Kwake Komwe . . .*

97 Ganizo lokongola bwanji ili liri! Tiyeni tingowerenga mopitirira miniti yokha. Ine ndikufuna ndifike pansu apa makamaka ku ndime ya 12, ndi ya 13, ya 14:

*Kuti ife tikhale otamanda ulemerero wake, amene poyamba anakhulupirira mwa Iye.*

*Amene inunso munamukhulupirira, zitatha zimenezo inu munamva mawu a choonadi, ndi uthenga wa chipulumutso chanu: mwa amene . . . pambuyo . . . inu munakhulupirira, inu munasindikizidwa ndi Mzimu woyera wa lonjezo,*

<sup>98</sup> “Pambuyo pokhulupirira.” Oh, m’bale wanga wa Baptisti, inu munganene bwanji kuti Izo siziri chomwecho? Inu mumati mumalandira Mzimu Woyera *pamene* inu mukhulupirira? Iwo anati, “*Mutatha* kukhulupirira ndiye inu munasindikizidwa ndi Mzimu Woyera walonjezo.” Zindikirani:

*Amene ali chikole cha cholowa chathu, kufikira  
mawomboledwe a cholowa chake chogulidwa, ku  
chiyamiko cha ulemerero wake.*

<sup>99</sup> Tsopano, ife tikupeza ndiye kuti *chisindikizo* chimatanthauza kuti “ndi chinthu chotsirizidwa ndi Mulungu, icho chakhazikitsidwa kale.” Ndipo wokhulupirira aliyense anasindikizidwa ndi lonjezo ili kuyambira pachiyambi, pakuti asanayikidwe maziko a dziko lapansi, ife tinakonzedweratu ku kukhazikitsidwa kwa ana. Dziko lisanayambe nkomwe! Oh, chiyembekezo chotani. Izo zimatipangitsa ife kupuma mokhazikika ndi motsimikiza. Nangula ku moyo umene sumasunthidwira uku ndi uko, koma wozikika mwa Khristu, chiyembekezo chimene chiri chotsimikizika. “Anatikonzeratu ife asanayikidwe maziko a dziko lapansi, ku kukhazikitsidwa kwa ana mwa Yesu Khristu.” Oh, zopambana bwanji! Ndikuzikonda zimenezo: “ntchito yomalizika” ndi Mulungu.

<sup>100</sup> Tsopano, ndiloleni ine ndingobwereza Lemba lina kwa inu. “Onse amene Iye anawadziwiratu, Iye wawayitana; onse amene Iye anawayitana, Iye wawalungamitsa; onse amene Iye anawalungamitsa, Iye wawapatsa ulemerero.” Njira yonse kuyambira pachiyambi, Mulungu, mu malingaliro Ake aakulu opanda malire, anawuwneratu Mpingo Wake ndipo anawukonzeratu iwo ku kukhazikitsidwa kwa ana kudzera mwa Yesu Khristu, kuti awapatse iwo Moyo Wamuyaya pa mapeto a m’badwo. Ndi chinthu chokongola bwanji! M’bale Neville, izo zimangondipangitsa ine kumverera bwino kwambiri. Sichoncho inu? Oh, eya. Kukhazikitsidwa ndi Magazi a Yesu Khristu!

<sup>101</sup> Tsopano, zindikirani pamene ife tikupitirira. Tsopano, ife tikudziwa kuti ndi yomalizi-... Ife tinakonzedweratu ndi Mwanawankhosa. Mzimu Woyera ndiye Chisindikizo chathu. *Chikole* chimatanthauza “zambiri zikubwera.” Ife tangokhala chabe ndi *chikole* cha Ichu tsopano. Chikole ndi kungolipirako pang’ono (Oh, ndizokongola bwanji!), kulipirako pang’ono komwe kumagwirizira icho ndi kuchitchinjiriza ndi kuchizikitsa kuti pasakhale wina aliyense angachikhudze icho. Ndi chikole cha kukhazikitsidwa kwathu. Ameni. Mzimu Woyera tsopano ndiye chikole cha Mulungu mu mitima yathu (kusindikizidwa), kukhazikitsidwa kwa ana kukudikirira kumapeto kwa ulendo. Ana aamuna ndi aakazi a Mulungu!

<sup>102</sup> Tiyeni titembenuzire ku Lemba lina, mwamsanga ndithu, ine ndinalilemba pa tsamba lina ili apa. Aroma 8:22, ine ndikuganiza ndi zokongola. Tsopano, mu kuwerenga dzulo, ine

ndinakhala ngati ndinalemba Malemba angapo apa amene ine ndikufuna kuti ndilozereko.

*... ife tikudziwa kuti—ife tikudziwa kuti chirengedwe chonse chikubuula, ndi kumva zowawa pamodzi kufikira tsopano.*

*Ndipo osati icho chokha, komanso ifeeni nafenso, amene tiri nazo zipatso zoyamba za Mzimu, ngakhale ifenso tikubuula mwa ife tokha, kudikirira kukhazikitsidwa, kuti tikaone, kuwomboledwa kwa matupi athu.*

<sup>103</sup> Oh, inu mukuziona izo? “Chirengedwe chonse chikubuula,” anatero Paulo. Chirichonse chikubuula. Tayang’anani mitengo momwe imavutikira. Tayang’anani maluwa mmene amavutikira chifukwa cha moyo; kuti basi nkhungu iwagwetsere iwo pansi. Tayang’anani pa mitengo momwe imavutikira kunyamula nthambi zake kuti ziziyimba ulemerero kwa Mulungu. Mukuona? Chirichonse, chirengedwe chonse, nyama zonse, mbalame zonse, momwe iye amawulukira kuthawa kwa mdani mwamsanga ndi kuchokapo, chirichonse chikubuula. “Ndipo ife tokha,” anatero Paulo, “ife tikubuula, nafenso, ndi izo, pakuti ife tikuyembekezera chiwombolo cha thupi lathu.”

<sup>104</sup> *Koma tsopano! Tsopano!* Izo zinachita zaka zonsezi mpaka *pano! Tsopano* tiri ndi chikole cha cholowa chathu! Oh, mai! Kodi ife tiri ndi chiyani? Tiri ndi umboni wakuti Mulungu ali moyo. Tiri ndi umboni wakuti Mulungu ali nafe. Ife tiri ndi umboni wakuti Mulungu sanatisiye ife, kuti ife ndife ake ndipo Iye ndi wathu, chifukwa ife (mmatupi athu), ife tsopano timanyamula Mzimu Woyera wa Mulungu umene ukufuula, “Abba, Atate.” Ndipo palibe chomwe chingakhoze kuchotsa izo. Ife tazikika mwa Khristu.

<sup>105</sup> Tsopano, mitengo ilibe icho, chirengedwe chiribe icho, komabe ife tikubuulabe nazo limodzi chifukwa mpaka panobe ife sitinalandire chidzalo cha kukhazikitsidwa kwathu. Koma ife tiri nacho chikole cha izo, kuti ife tinatengedwa kuchokera ku zinthu za dziko ndipo tsopano takhala ana aamuna ndi aakazi a Mulungu. Kodi tiyenera kukhala anthu otani? Oh, mai, pamene ife tiganiza za zimenezo! Taganizani za izo!

<sup>106</sup> Tsopano tiri nacho chikole, mzimu wathu ukubuula chifukwa cha kukhazikitsidwa kwathunthu, koma tsopano tiri nacho chikole chake. Pamene tilandira Mzimu Woyera, ndi chikole cha kukhazikitsidwa kwathu kwathunthu kapena chipulumutso chathunthu. Oh, nzokongola bwanji! Ine ndimangozikonda izo. Chabwino.

<sup>107</sup> Ife tikudikirira chidzalo cha kukhazikitsidwa. Izi zidzachitika liti? Pa chiwukutsiro choyamba. Ndi pamene matupi athu adzasinthidwa kuchoka ku zorengedwa zoyipa zomwe ife tiri ndipo ife tidzakhala ndi thupi ngati thupi Lake

lomwe laulemerero, “Pakuti ife tidzamuona Iye momwe Iye aliri, ndipo ife tidzakhala ngati Iye.” Iye akadzawonekera, ife tidzawonekera mu chifaniziro Chake. Ife tidzakhala ndi thupi ngati Lake, thupi laulemerero lopatsidwa ulemerero, ndipo mayesero onse ndi zovuta za moyo zidzazimirira kukhala nkhangungu yaying’ono ndi kuwuluka kuti isakhaleponso.

<sup>108</sup> Ndipo makachisi a dziko lapansi awa amene ife tikubuulamo tsopano, ife tikuyembekezera chikole chimenecho—chikole chimenecho...kwa chipulumutso chokwanira mu chidzalo chake kuti chibwere. Koma tsopano mu makachisi awa a dongo ife tiri ndi Chinachake chimene chimatiuza ife kuti tawuka pakali pano. Amen. Kodi chikole ndi chiyani? Ndi kulipirira mwaheka komwe kumagwira icho, M’bale Dauch. Ndi chikole. Tsopano, nthawi ina pamene ife tinkakonda zinthu za dziko lapansi, nthawi ina pamene ife tinkachimwa ndipo tinkapita kulikonse nkumakachita zinthu za dziko lapansi, ndipo sitinkasamala za Mulungu, ife tinali olekanitsidwa ndi Iye, opanda Mulungu, opanda Kristu, mu dziko lapansi; tsopano, Mulungu anatumiza Mzimu Wake Woyera ndipo kudzera mu zimenezo ife takwezedwa mmwamba kuchoka ku zinthu zimenezo. Tsopano ife tiri nacho chikole, mwakuti ife tikudziwa kuti tadutsa kuchoka ku imfa kupita ku Moyo. Amen!

<sup>109</sup> Apa, pamene ine ndimayesera kusonyeza izi monga *chonchi*. Apa ndi pamene wochimwa wamba amathamangira, pansu apa pansu. Tsopano, Mkhristu amapita pamwamba pang’ono kuposa apa, iye amakwera pamwamba pa zinthu zonse izo. Ndicho chikole cha chipulumutso chake.

<sup>110</sup> Tsopano, kuti inu mukhoze kudziwa pamene...zomwe masomphenya amachita kwa inu. Kotero ndithandizeni ine, Mulungu pokhala woweruza wanga, ine sindimalinga kuti ndikhale ndi wina. Ngati izo zitero, ine ndizisunga izo kwa inemwini, mwaona, chifukwa ine ndikuwona zomwe iwo amachita. Anthu siali okonzekera utumiki woterowo, kotero inu mumangoyenera kuzilola izo kuti zipite, inu mukuona, pitirirani kubwerera kuno. Koma ngati ine ndidzabweranso ku ntchito kachiwiri, ine ndidzakhala mlaliki. Koma tayang’anani apa. Pa izi apa, kubwerera mkati umu, m’mwamba umu, inu mumakwera mu Ammwambamwamba awa mmwamba umu. Inu mumakhala komweko mu madera awo kumeneko. Inu mumapita kupyola chirichonse chimene munthu angakhoze kuchiganizira, kupitirira chirichonse cha zinthu zimenezo. Ndipo izo zimakubweretsani inu mu madanga amenewo uko.

<sup>111</sup> Koma, inu mukuona, tsopano ife tiri nacho, mwa Mzimu Woyera, chikole cha cholowa chathu chifukwa ife takwezedwa kuchokera ku zinthu za dziko; ndipo ife tikukwera limodzi ndi dziko, koma ife tiri pamwamba pa dziko! O M’bale Neville,

Mulungu atichitire chifundo ndipo apereke kwa Mpingo wa Mulungu wamoyo . . .

<sup>112</sup> Pamene ife tidzafika pa malo oganiza kuti mpingo, mpingo wokongola, kuti, “Tikuyesera kumafanizira ndi zinthu za dziko lapansi. Tikuyesera kukhala ndi timu yabwinoko ya basketball kuposa yomwe iwo ali nayo. Tikuyenera kukhala ndi a—chimango chabwinoko. Tikuyenera kukhala ndi masewera abwinoko a bunco. Ife tikuyenera kukhala nazo zabwinoko *izi* ndi *izo*, kapena *izo*.” Bwanji, ife tingawufanizire bwanji Iwo ndi kukongola ndi kunyezimira kwa dziko lapansi? Ife sitiri . . . Uthenga si *kunyezimira*; Ndi *kuwala*. Pali kusiyana pakati pa kunyezimira ndi kuwala.

<sup>113</sup> Mwaona, ife timangoyendayenda, monga ine ndanenera, kutenga umodzi—mtembo umodzi kuchoka ku motchale ina kupita ku inzake, kusintha mamembala ndi zinthu monga choncho. Chabwino, kodi *izo* zimatichitira ife ubwino wanji? Ndipo ife tikuyesera kuzipanga *izo* zonyezimira, zipilala zazikulu zabwino, malo akulu abwino kwambiri. “Ifi tikuyenera kukhala ndi wina wabwinoko kuposa wa Methodisti kapena wabwinoko kuposa wa Baptisti, ndipo ife tonse tikuyesera kupikisana ndi Akatolika, ndipo ife tiri ndi masewera a bunco ndi maphwando ndi mgonero ndi zosangalatsa, ndi chirichonse.”

<sup>114</sup> Mpingo sungafanane konse ndi dziko. Kodi zingatheke bwanji inu ndi zosangalatsa za mpingo wanu kuti zifanane konse ndi Masonic Lodge kapena—kapena aliynse wa anthu amene angakhoze kusangalatsa? Amenenewo ndi mabwalo awo. Musayesere kupita pa mabwalo awo.

<sup>115</sup> Koma ife tiri nacho Chinachake chomwe iwo alibe! Ife tiri naye Yesu. Asiyeni iwo abwere kuno ngati iwo akufuna chinachake. Khalani mwa Khristu. Tiri ndi Yesu. Iwo sadzatero . . . iwo sangakhale naye Yesu mpaka iwo atabwera kuno. Ndipo ife tikapita kumeneko, tachoka pa mfundo Zake.

<sup>116</sup> Musayesere kunyezimira. Walani! Ndipo inu simungakhoze kuwala, inu muyenera kuwulola Iwo uwale kudzera mwa inu. Mukuona?

<sup>117</sup> Kachiphaniphani kakang’ono, iko sikamawala chifukwa choti kakufuna kuti kawale; chifukwa iye *amawala*, pali chinachake mwa iye chowala. Icho chiri mwa iyemwini, ndi iyemwini akuchita *izo*, chinachake mkati mwa iye chikungomuwalitsa iye mopitirira.

<sup>118</sup> Chabwino, umo ndi momwe ziliri ndi Mzimu Woyera. Sitiyenera kukhala apadera, kukhala osiyana, kukhala china chirichonse, ingodzimasulani ndi kumakhala moyo waumulungu ndi kungomulola Mulungu kukhala moyo kudzera mwa inu. Izo zidzawala kwa Uthenga. Mukuona? Osati kunyezimira; *kunyezimira*, *izo* zimapangitsa anyani kulumpha pa zinthu monga choncho, chirichonse chonyezimira.

Inu mukudziwa, iwo nthawizonse amalumphira chinachake “chimene chiri chonyezimira.” Koma *kuwala* ndiye “kufewa, kukoma kwabwino kwa—kwa Mzimu Woyera.”

<sup>119</sup> Tsopano ife tikuyembekezera chiwukitsiro chimenecho. Chabwino, tsopano, kodi inu mukumvetsa? Nenani, “Ameni,” ngati inu mukutero, chimene ine ndikutanthauza pa kunena “chikole.” [Osonkhana akuti, “Ameni.”—Mkonzi.] Ife takhala. . . Ife—ife tikudziwa tadutsa kuchoka ku imfa kupita ku Moyo chifukwa ife takwezedwa pamwamba. Ife takwezedwa pamwamba osati mwa ife tokha, koma kukwezedwa kuchoka ku zinthu za dziko, mwakuti ife timamukonda wina aliyense. Ndipo Mulungu amatikonda ife, ndipo ife tikudziwa izo. Ndipo ife timayang’ana miyoyo yathu ndi kuwona kuti Iwo ndi Mzimu Woyera, chifukwa ife sitimasamalanso za zinthu za dziko lapansi. Mwaona? Ndi zimenezotu. Bola ngati inu mumakonda dziko kapena zinthu za mdziko, ndiye chikondi cha Mulungu sichiri mwa inu apobe. Mukuona? Koma bola ngati inu muli pamwamba pa zimenezo, ndiye inu mumadziwa kuti muli ndi cholowa chanu, mwaona, inu—inu muli panjira yanu ya kuchiwombolo chanu chathunthu.

<sup>120</sup> Ndipo, tsopano, izo sizibwera, inu mukuona, mpaka ife titakhala nazo poyamba. . . Choyamba ife tikuyenera kumuona Yesu. Ndipo pamene Iye abwera, ndiye ife tidzakhala ndi thupi monga thupi Lake ndipo ife tidzapangidwa monga Iye. Chabwino.

<sup>121</sup> Tsopano, ife tikuwona chinachake chimene chinatayika apa, chifukwa Baibulo linanena chomwecho, ndipo, mu Bukhu umu amene—amene watiwombola ife. Kodi ife tawomboledwa ku chiyani? Chinachake chomwe tikuyenera kuti tinachitaya. Musanawomboledwe, pakuyenera kukhala chinachake chimene chinatiwombola ife kutibwezeretsa. Ndipo cholowa chonse chimene ife tinali nacho chakhala chiri—chawomboledwanso. Ndiye ife tiyenera kuti tinali nacho chinachake nthawi ina chimene ife tiribe tsopano, koma Mwanawankhosa uyu anabwera kuti adzawombole. Mukuona? Ife tinali ndi chinachake chimene ife tinatayikako.

<sup>122</sup> Tsopano zindikirani. Ife tinataya chiyani? Chabwino, izo zinaperekedwa kwa Adamu kuti akhale nawo Moyo Wamuyaya, nthawi zonse pamene iye ankadya za Mtengowo iye anali nawo Moyo Wamuyaya. Ndipo ife tikuzindikira kachiwiri kuti Adamu anali. . . iye—iye analandira dziko lapansi. Iye anali. . . ngati mulungu wamng’ono pa dziko lapansi. Dziko lapansi linali lake. Chirichonse chinapatsidwa mdzanja lake, iye ankakhoza kuchita nalo chirichonse chimene iye ankafuna. Iye analipatsa dzina ilo, ndipo analitchula ilo, ndipo anachita chirichonse chimene iye ankafuna kuchichita. Iye ndithudi anali mwana wa Mulungu.

123 Tsopano, mu kugwa, Adamu analanditsa chikalata chaumwini kwa ilo. Iye anachipereka icho kwa Satana. Satana anatenga chikalata chaumwinicho. Adamu anali wozengereza kwambiri, ndipo iye sanawombole maufulu ake chifukwa iye sakanatha kuwombola maufulu ake. Koma Satana, yemwe siali mwini wake wovomerezeka, koma iye ali nalo ilo, iye ndi mulungu wa dziko lino. Baibulo linanena chomwecho. Iye ali nalo ilo. Osati chifukwa kuti iye—kuti iye—iye movomerezeka analipeza ilo, koma iye ali nalo ilo. Tsopano kodi inu mukuzimvetsa izo? Satana ali nalo ilo, iye akuligwira ilo mu dzanja lake. Imfa ili mdzanja lake, dziko liri mdzanja lake, dziko lapansi ndi lake, fuko lirilonse ndi lake, iye amayendetsa ndi kulamulira dziko lonse lapansi ndi chirichonse mu dziko lapansi. Satana amatero!

124 Koma tithokoze Mulungu kuti sitiri a dziko lapansi. Mukuona? Kotero pamenepo—ndi inu apo. Mukuona? Ndipo ife tiri. . . Ine sindikutanthauza Mpingo; iye salamulira Mpingo. Iye amangolamulira dziko lapansi. Iye anati iwo anali ake, ndipo iye ndi mulungu wa dziko lapansi. Yesu anati iye anali, ndipo iye ali. “Iye ndi mulungu wa dziko lapansi lino, wachititsa khungu maso a anthu,” mulungu wa dziko lapansi lino. Iye ndi Mulungu wa Kumwamba. Ndipo tsopano iye moyenerera alibe ili. Iye siali mwini wake.

125 Koma iye anakana. . . ndipo Adamu analanditsa chikalata kwa ilo, kwa ilo, zinthu zonse izi zomwe ife tiri nazo, Moyo Wamuyaya ndi kulandira kwa dziko lapansi. Yesu anati, mu Mateyu 5, “Odala ali ofatsa chifukwa adzalandira dziko lapansi.” Mukuona? Tsopano, ife tiribe ilo tsopano.

126 Ndipo, penyani, ilo silinali la kwa Adamu kapena iliyonse ya mbewu zake. Mbewu ya Adamu mwamtheradi inataya chirichonse, nayonso. Iyo si mbewu ya Adamu. Ziribe kanthu momwe ife timayesera kulikongoletsa dziko ili, ndi mochuluka bwanji ife timayesera kupanga nyumba zazikulu zabwino ndi zinthu, ilo si la mbewu ya Adamu apobe. Ayi, bwana. Ilo silinapite kwa mbewu ya Adamu, ayi, bwana, chifukwa Satana anatenga ilo, chivindikiro ndi mbiya. Kulondola! Pakuti Adamu analilanditsa ilo.

127 Tsopano, oh, mai! Inde, zinthu zochuluka kwambiri zikhoza kunenedwa. Ine—ine sindikufuna basi kuti nditenge nthawi yochuluka kwambiri tsopano, kotero ife tiyenera, kuti tibatize. Chabwino.

128 Iye ali nalo ilo koma iye siali mwini wake wovomerezeka, Satana amatero. Pamene mwiniwake wovomerezeka—mwini wake wovomerezeka—mwini wake analitaya ilo, pali njira imodzi yokha yomwe ilo lingawomboledwere. Tsopano, izo ziri mwa wachibale wapafupi, ndi mmodzi yekhayo amene

angakhoze kuliwombola ilo movomerezeka. Tsopano, ndithudi, izi ife tiri nazo mu kubadwa kwa unamwali kwa Yesu Khristu.

<sup>129</sup> Tsopano, ine ndikufuna kuti ndinene chinachake apa. Chinthu choyamba chimene ife tikufuna kuti tibwerereko, ndi, ngati ife titi tibwerere mu—mu Chipangano Chakale apa, Ine ndikukhulupirira ine ndinazilemba izo apa penapake, Levitiko 25. Mu Levitiko 25:23 ndi 24, inu mukhoza kupeza malamulo a chiwombolo, inu amene mukulemba. Kuwombola chirichonse pamene munthu... Pamene Mulungu anapereka kwa Israeli lake... anagawa dziko lake kudzera mwa Yoswa, fuko lilirilonse ndi munthu aliyense anapatsidwa malo kumene ana ake anadzalandira cholowa chake—chuma chake.

<sup>130</sup> Tsopano, ngati munthu uyu anasauka ndipo anataya chirichonse kupereka kwa munthu wina, ichi... ndipo njira yokhayo yomwe icho chikanakhoza kuwomboledwera ikanakhala wachibale wapafupi. Koma potsiriza icho chikuyenera kubwerera. Munthu uyu wangochitenga icho kwa nthawi inayake. Chikuyenera kubwerera kwa mwini wake wapachiyambi. Kulondola! Icho chikuyenera kubwerera kwa mwini wake wapachiyambi. A... ngati anali ochokera kunja kwa fuko la Yuda, ngati icho chinali... Ngati iye anali kumeneko ndipo ichi chinapatsidwa kwa abambo ake, ndiye icho chinali kwa iye, kapena wachibale wina wapafupi akanakhoza kuchitenga icho. Koma, tsopano, palibe wina akanakhoza moyenera... Iwo akanakhoza kuchigwira icho, iwo akanakhoza kutenga chikalatacho pa icho. Iwo akanakhoza kutenga chikalatacho mpaka ngongole italipidwa, koma munthu woyenera akabwerapo, munthu amene... .

<sup>131</sup> Tinene, mwachitsanzo, ngati ine ndinali ndi gawo la katundu ndipo ndinamutaya, ndipo ine ndinamugulitsa iye kwa M'bale Neville yemwe ali wa fuko lina, la Yuda, kapena mwinamwake ndinamugulitsa iye kwa mlendo. Ndipo iye anali mwini wake wovomerezeka, iye anali mwini wake, iye akanakhoza kubwera mmenemo ndi kudzalimapo ndi kuchotsapo katundu pa izo, ndi zina zotero, koma kwenikweni iye anangogwira chikalatacho. "Iye sakanakhoza kukhala mwini wake," limenelo linali lamulo mu Israeli. Tsopano inu muwerenge mu—muwerenge mu Levitiko 25, ndipo muwona kuti iwo sakanatha kukhala eni ake; iye basi *anangogwira* icho.

<sup>132</sup> Chabwino, tsopano, mwachitsanzo, mwana wanga ankafuna... Billy, kumbuyo uko, ankafuna kuti atenge anga... kubwera kudzagula malo awa. Chabwino, ndiye, ngati mlendo kapena M'bale Neville kapena—kapena munthu wina anali mwini wa iwo, anali kusunga chikalata kwa iwo... Tsopano, ngati uyu anali wachibale wanga wotsatira, anali wachibale wanga wamagazi, iye sakanakhoza kuchigwira icho mopitirira. Ayi, bwana. Iye amayenera kuchipereka icho, inde, bwana,



pamene mtengo umenewo walipiridwa, pamene anampatsa iye, titi, madola twente faivi sauzande kwa gawo la malo.

<sup>133</sup> Chabwino, ndiye, nkuti, M'bale Tony angabwere ndi kuti, "M'bale Neville, ine ndigula malo a M'bale Branham." Iye sakanakhoza kuchita izo.

M'bale Neville nkuti, "Ayi, bwana, ine sindikufuna kuwagulitsa iwo."

"Chabwino, mungapereke chiyani kwa iwo?"

"Twente faivi sauzande."

"Chabwino, ine—ine ndikupatsani sarte faivi sauzande. Ine ndikupatsani *mwakuti ndi mwakuti.*"

"Ine sindikusamala zomwe inu mukufuna. Ine sindikufuna kuwagulitsa iwo, ine ndiwasunga iwo."

<sup>134</sup> Koma Billy Paul akhoza kubwera ndi kuti, "Ndikufuna chuma cha Adadi anga, nayi twente faivi sauzande yanu." Iye ankayenera kuwapereka iwo. Ndiko kulondola, chifukwa ilo linali lamulo.

<sup>135</sup> Oh, Aleluya! Hmm! Ine ndikuyembekeza inu Akhristu mukuziwona izo. Ndife mchere wa dziko lapansi. Mulungu anapereka izi kwa ana Ake. Iye anatipatsa ife ulamuliro pa chiredgedwe chonse, nyama zonse, zamoyo zonse kulikonse. Koma Adamu, atate wathu, anazipereka izo kwa Satana. Koma izo zikubwerera kuti? Kwa Mwini wovomerezeka, Mulungu Yemwe anazipanga izo. Amen!

<sup>136</sup> Nzosadabwitsa Yohane anati iye "analira mowawa," pakuti sanapeze munthu woyenera kuliwombola ilo. Munthuyo ayenera kukhala woyenera. Yohane anati, "Ine ndinalira mowawa pamene panalibe mmodzi yemwe anali wokhoza kutenga Bukhulo kapena kuyang'ana pa Ilo kapena kumasula zisindikizo zake." Iye anati, "Ayi... Palibe munthu Kumwamba, palibe munthu pa dziko lapansi, palibe munthu pansa pa dziko lapansi, palibe munthu kulikonse."

<sup>137</sup> "Palibe munthu." Tsopano, iye sananyoze konse Angelo. Kumbukirani, dziko lapansi ili silinaperekedwe kwa Angelo. Ndi cholowa cha munthu. Gabrieli anali woyenera, ndithudi; winawake anali woyenera, Mikaeli akhoza kukhala kuti anali. Osati ngati... Iye akhoza kukhala anali woyenera kuti achite izo. Koma panalibe munthu woyenerera. Mukuona? Ndipo Yohane analira mokweza.

<sup>138</sup> Wina anati, "Chifukwa iye anadzipeza yekha kukhala wosayenera." Izo siziri choncho. Munthuyo anali pansa pa chikoka cha Mzimu Woyera, iye sakanakhoza kulakwitsa moteromo. Koma iye—iye anali... iye—iye anali—iye anali... Sianali iye yekha woyenera, iye sakanakhoza kupeza aliyense woyenera.

139 Kotero basi ndiye iye anati, “Panabwera mkulu kapena mngelo wamphamvu, anati, ‘Usalire, pakuti Mkango wa fuko la Yuda,’” (Ameni!) “‘Muzu wa Davide, Iye wapambana!’” Ameni! “‘Wagonjetsa,’” mwanjira ina. “‘Iye ndiwoyenera kulitenga Bukhulo!’” Ameni.

140 Kumbukirani, iye anali asanamuwone Iye mpaka nthawi iyi. Chifukwa chiyani? Iye anali atakhala pa... atakhala pa Mpandowachifumu mmenemo, Mpandowachifumu wa Mulungu. Iye anali mkati mwa malo opatulika. Iye anali asanamuwone Iye mpaka nthawi imeneyi, kotero Yohane anali kuymbekazera kuwona a—Mkango ukutulukira, koma iye anawona Mwanawankhosa!

141 Ndi zimenezotu, abale. Kudzera mu kufatsa, kudzera mu kukoma, kudzera mu Mzimu Woyera mmene ife timagonjetsa. Osati chimphona china chachikulu chaluntha champhamvu, koma iye amene angakhoze kudzichepetsa yekha ndi munthu amene amagonjetsa. Munthu yemwe angakhoze kukankhidwa ndi kukhalabe wantchito wa Khristu, ndiye mgonjetsi.

142 Tsopano, iye anati, “Iye wapambana. Ndipo Iye ndi woyenera kutenga Bukhulo ndi kulitsegula ilo ndi kumasula zisindikizo zake.”

143 Tsopano, ife tipeza pakapita kanthawi, mwinamwake osati lero, koma chimene zisindikizo seveni izi zanyamula, zomwe izo zinachita.

144 Tsopano, tiyeni titengepo pang’ono pa “chiwombolo.” Asanakhoze—munthu uyu asanakhoze... kukhoza kuwombola, chinthu choyamba, iye ankayenera kuti akhale woyenera, iye ankayenera kuti akhale mtundu woyenera wa munthu. Kotero izi zinakwaniritsidwa pamene Yesu Khristu anabadwa, kubadwa kwa unamwali, pakuti Iye anali Mulungu. Iye anali Mulungu Mwiniwake anapanga munthu, Iye anali Mulungu mu thupi la munthu. Iye ankayenera kuti akhale woyenera; ndipo Magazi aunamwali a Yesu Khristu anamupanga Iye kukhala woyenera. Tsopano, ife tikupeza kuti, ngati inu mukufuna kuti mupite ku Lemba la izo, la Petro Woyamba 1:18 mpaka 20, ngati inu mukusunga Malembawo. Iye ankayenera kukhala woyenera. Ndipo Iye anali, chifukwa Iye anadzitengera pa Iye mawonekedwe a munthu. Iye anasandulika munthu, Mulungu anakhala wachibale kwa ife. Ndipo pamenepo ife tikupeza ndiye gawo lokongola la Mulungu Yehova kupangidwa thupi ndi kukhala pakati pathu monga Iye woyenerayo. Ameni.

145 “Iye anapambana.” Mulungu anatenga mawonekedwe a thupi la munthu, Iye anabwera ku dziko lapansi, anabadwa khanda laling’ono ndipo anayenda pakati pathu. Ndipo kudzera mu Magazi Ake Oyera Iye anapambana.

146 Tsopano, mu Chipangano Chakale, momwe munthu ankayenera kulengeza zake zomwe, kodi iye ankachita chiyani?

Iye ankamutenga mkulu, akulu teni, ndipo ankapita ku chipata ndipo ankafotokozera chimene iye ankachita, kuti awombole chimene iye anali atataya, ndipo ankasonyeza yemwe iye anali, ndipo iye ankachitira umboni. Ife tikupeza nkhani yokongola apa (Monga ine ndinali ndi ka pepala kakang'ono komwe ndinalamba apa kuti...kotero ine ndisakhoze kuyiwala izo, pokhala wamanjenje mmawa uno.) pa Rute, wachibale ndi Boazi. Ife tinadutsamo osati kale kwambiri. Ine ndikufuna inu muzindikire magawo atatu tspano a kupumula uku.

<sup>147</sup> Ine ndikufuna inu muzindikire kupumula kwa Mpingo, ndendende basi chinthu chomwecho. Tspano, penyani. Malo oyamba omwe ife tikupeza, monga ife tonse tadutsa mu ulaliki umenewo, *Wowombola Wachibale*, Mulungu anapangidwa thupi ndi cholinga choti akhale Wowombola. Iye anali Mmodziyo apa mu mutu wa 5—mu mutu 5. Anati:

*Ndipo panalibe munthu kumwamba, kapena padziko lapansi, kapena pansu pa dziko, akanatha kutsegula bukhulo, kapena kuyang'ana pa ilo.*

*Ndipo ndinalira kwambiri, chifukwa sanapezeke munthu woyenera kuti atsegule Bukhulo kapena kuwerenga—kapena kuwerenga bukhulo, kapena kuyang'ana pa ilo.*

*Ndipo mmodzi wa akuluwo ananena kwa ine, Usalire: tawona, Mkango wa fuko la Yuda, Muzu wa Davide, wapambana kuti atsegule bukhulo, ndi kumasula zisindikizo zisanu ndi ziwirizo pa ilo.*

Iye ndi Ameneyo, Iye ndi Ameneyo yemwe tikumufunafuna.

<sup>148</sup> Zindikirani momwe Rute anachitira...momwe...ndi Naomi, Boazi ndi chithunzi changwiro basi. Momwe Naomi mu nthawi ya njala anasiya mpingo, anachoka mu dzikolo, anapita ku dziko la Moabu kukakhala kumeneko ndi kukayenda kumeneko. Iye anataya zonse zomwe anali nazo. Ndipo pamene iye anachoka, mwamuna wake, Elimeleki, anamwalira pamene iwo anali kumeneko, kotero izo zinapangitsa kuti cholowa chake chigwere aliyense. Ndiye pamene ife tibwera...pamene iye anabwerera, iye akubwera ndi mkazi wamasiye wokongola wachimoabu ndi iye. Ndipo pamene Boazi anamuwona mkazi wamasiye uyu, choyimira cha Khristu, iye anakopeka naye. Ndipo iye anamkonda mkaziyo. Kotero, iye ankayenera kuti awombole, njira yokha yomwe iye akanamupezera konse iye kuti akhale mkazi wake inali kuwombola chimene m'bale wake, Elimeleki, anataya.

<sup>149</sup> Ndipo kotero ndiye iye anamufunsa m'bale wake wina ngati iye akanati awombole izo, mmodzi wapafupi kwambiri kuposa iye, ndipo iye sakanakhoza kuchita izo. Kotero iye anapita pansu kukapanga chitsanzo changwiro cha malamulo a Mulungu. Iye anapita ku zipata ndipo anavula nsapato yake, ndipo anati,

“Zidziwike lero kuti ndawombola zonse zimene Naomi anali nazo. Zonse zomwe ali nazo, zonse zomwe Elimeleki (m’bale wanga) anataya, ndine wachibale wotsatira tsopano, ndipo ndine amene ndingathe kuwombola izo kotero ine ndabwera kuti ndidzazitenge izo. Ngati pali mwamuna aliyense pano yemwe angasonyeze chifukwa cholungama, kapena aliyense wapafupi kuposa ine, mulole izo zidziwike.” Ndipo aliyense anatseka pakamwa pake. Kotero iye anavula nsapato yake ndipo anayiponya iyo ngati umboni, “Ine ndawombola zonse zimene m’bale wathu, Elimeleki, anali nazo.” Bwanji? Iye anali wachibale. Iye anali wowombola wachibale. Oh, ndi zokongola bwanji izo! Ndi nkhani yokongola kwambiri.

<sup>150</sup> Ndiyeno, nthawi yonse, Rute anali akupumula ndi kuyembekezera kuti afufuze momwe izo zidzachitikire. Ndiye iye akubwerera, panalibe amene akanakhoza kupereka umboni wotsutsa izo. Iye anabwerera ndipo anamutenga Naomi... ndipo anamutenga Rute, mtsikana wokongola wa ku Moabu, ndipo iwo anakwatirana nakhala pa chuma ichi. Nkhani yokongola bwanji!

<sup>151</sup> Pali magawo atatu a Rute. Rute—Rute, *kusankha*; iye angaganiza ngati iye angapange lingaliro kapena ayi, kuti abwerere ku dziko la kwawo (basi monga Mpingo). Rute, *kutumikira*; pamene iye anapita kunja kukakunkha. Rute, *kupumula*; ndicho chimene Rute akuchita tsopano (Mpingo). Tsopano Rute, *analandira mphotho*; tsopano ndi pamene, kapena, chinthu chotsatira chimachitika (ndi mphotho ya Mpingo).

<sup>152</sup> Tsopano, ife sitingathe... Ine ndiribe nthawi, chifukwa inu muli ndi utumiki wa ubatizo ndipo ndi kotala itadutsa leveni tsopano. Koma mwinamwake ife tidzatenga izi Lamlungu likudzali kapena Lamlungu lina mtsogolomo, Ambuye akalola. Ndipo ine ndikufuna kuti ndizitengere izi panso apa, kuti ndiwonetse nyanga seveni izi ndi maso seveni, ndipo ndendende zisindikizo seveni zimenezo, mautumiki seveni, angelo seveni a mpingo, nyenyezi seveni, se- . . . Oh, zochepa zokhazo . . .

<sup>153</sup> Ndipo pomwe pano zikumangiriza chinthu chonsecho pamodzi. Inde, bwana. “Ankayenera kukhala oyenera,” kotero Yesu ali woyenera. Pa kubweranso Kwake tidzakondwa kwathunthu ndi chidzalo chonse cha madalitso achiwombolo. Ofatsa adzalandira dziko lapansi. Amuna ndi akazi adzakhala atabwerera: ana aamuna ndi aakazi a Mulungu. Ndipo gawo lathunthu la Zakachikwi lidzayamba. Ndi chinthu chokongola bwanji!

<sup>154</sup> Ndipo mngelo wamphamvu ndi liwu lalikulu, akulengeza, “Ndani ali woyenera? Ndani angathe kuchita zimenezi?”

<sup>155</sup> Kenako mkulu anati, “Usalire, pakuti Mkango wa fuko la Yuda, Iye ali woyenera ndipo Iye wagonjetsa.”

156 “Ndipo Iye anatenga Bukhulo ndipo analitsegula Bukhulo namasula zisindikizo zake.” Iye sananene zimene zinachitika kwa iwo. Pamene ife tidzakhudza zisindikizo seveni zimenezo zikutsegulidwa kudzera mu Baibulo, penyani chimene chinachitika. Momwemu mu Bukhu ili la zisindikizo seveni lomwe ife tikulowamo tsopano, liri ndi chinsinsi chonse cha madalitso a chiwombolo cha Mulungu. Kumbukirani, Iye ndi Mwanawankhosa, Iye ndi Mmodzi yekhayo amene analiwombola ilo. Ndipo, kumbukirani, ilo ndi losindikizidwa kuseri kwa Bukhulo, losalembedwa mkati mwake. Ilo lasindikizidwa kumbuyo, ndipo ndi losalembedwa mkati mwake. Ndipo Iye anali Mmodzi yekhayo amene anali wokhoza ngakhale kutsegula Bukhulo kapena kuwulula Bukhulo kapena kuwulula zisindikizo, Mmodzi yekhayo amene akanakhoza kuchita izo.

157 Kotero ichi ndi chinthu chimodzi, iwo akhoza kukangana za izi mkati muno, za zomwe izo ziri, koma Iye ndi Mmodzi yemwe mwaumulungu amawatanthauzira Iwo. Koma kumbuyo kuno palibe amene angakhoze kuchita izo. Izo ndi za Iye ndipo Iye yekha, ndipo Iye ndi Mmodzi yemwe angakhoze kuwulula zinsinsi zisanu ndi ziwiri zimenezo. Ndipo penyani momwe chidutswa chirichonse cha izo chiri pa chiwombolo, momwe Mpingo unawomboledwera ndi chomwe chiti chidzakhale kuwombolako.

158 Oh, tiyeni ife tingomukonda Iye ndi mitima yathu yonse, tichite zonse zomwe ife tingakhoze.

159 Wolemba wina anali kulemba nkhani. (Ine ndisanatseke basi ndi kubwezera msonkhano kwa M'bale Neville.) Kodi mukusangalala ndi Chibvumbulutso? Oh, ine ndikungozikonda izo. Ife tangotenga pafupifupi ndime zitatu za izo mmawa uno, koma ife tidzazitenganso izo kachiwiri. Zindikirani. Ife basi . . .

160 Wolemba ankalemba bukhu lokhudza mtsikana wina amene ankayesetsa kuti amupeze Mulungu.

161 Ndipo nthawi zambiri zomwe ife timamusaka Mulungu ndi kumufunafuna Mulungu, ndipo ngati Mulungu anali paliponse ndipo inu . . . Iye anali ndi wopambana wawukulu . . . Chabwino, ngati Iye anali ndi mpandowachifumu wopambana wawukulu utakhala pamwamba apa penapake, aliyense akanakhulupirira mwa Mulungu pamenepo. Ngati Mulungu angakhale pa mpandowachifumu wawukulu pano penapake; nkuti, “Iye akukhala mu mzinda winawake uwu ndipo apa Iye ali. Uyu ndi Mulungu ndipo inu mupite kwa Iye. Iye angakhoze basi” [M'bale Branham akukhwatchitsa zala zake—Mkonzi.] “kutembenuza izo monga *choncho*,” bwanji, aliyense akanamukhulupirira Iye. Pamenepo chikhulupiriro chikanakhala chopanda ntchito. Ife sitikanakhala ndi chikhulupiriro chirichonse pamenepo, inu mukuona, izo zikanakhala zimenezo. Izo zidzakhala mu

Zakachikwi, koma tsopano Iye akuyitana ndi kuyesera kuti awapeze iwo amene... Zikuwoneka zachinsinsi ndi zakuda, ndipo, inu simukudziwa momwe mungachitire izo. Koma mwa chikhulupiriro ife timazikhulupirira Izo! Ife timakhulupirira. Ichi ndi chifukwa chake izi ziri. Inu mukumvetsa zimenezo, M'bale Elmer? Mukuona? Kuti...

<sup>162</sup> Tsopano, ngati Mulungu akhala pa mpandowachifumu. Ndipo anati, “Bwanji, apa Iye... apo Iye... apa pali Mulungu. Iye amakhala kumusi ku malo enaake, ife tidzapita kumeneko.” Ndi kunena, “Wokonedwa Bwana, Mulungu, kodi inu mungachite izo?”

“Inde, ine ndidzachita zimenezo.” “Psst!” Ndipo izo zikanachitika, mwaona. “Chabwino, ndithudi, ameneyo ndi Mulungu. Mukuona? Mai, ife tikuwona izo.” Kotero sipakanakhala kusowekera... chikhulupiriro chikanakhala chopanda ntchito. Chikhulupiriro sichabwino ngati muli wotsimikiza.

<sup>163</sup> Bwanji ngati munthu aliyense mu dziko lino akanakhala Mkhristu? Bwanji ngati aliyense anali a—Mkhristu wodzazidwa ndi Mzimu? Bwanji, ife sitikanasowanso chikhulupiriro chirichonse, sitikanasowa chikhulupiriro chirichonse nkomwe. Ndipo chikhulupiriro ndicho chenicheni—ndi chinthu chomwecho chimene ife timapulumsidwa nacho, ndicho chikhulupiriro. Ndipo ndicho chifukwa payenera kuti pakhale ena osagwirizana nawo Iwo, kotero kuti ife tikhoze kuchita chikhulupiriro. Kodi mukumvetsa izo tsopano? Inu mukuyenera kukhala ndi mbali inayo. Mukuona? Inu mukuyenera kukhala ndi mkazi woyipa kuti amupangitse weniweniyo kuyima molondola. Mukuona? Pakuyenera kukhala bodza kuti lipangitse Choonadi kukhala chenicheni ndi kuchipanga Icho kuti chiwale bwino. Ngati chirichonse chikanakhala Choonadi, Icho chikanakhala chawamba kwambiri, mwaona. Mwaona? Koma, inu mukuona, ndi chinachake chachifumu, ndi chinachake chenicheni, pamene Choonadi ndi chikhulupiriro ndi zina zotero. Tsopano, ndi ife apo.

<sup>164</sup> Tsopano, ife tiyenera kukhala ndi zabwino ndi zoyipa izi. Umo ndi momwe zimakhallira. Inu mumayenera kukhala ndi masiku abwino kuti musangalale... kapena masiku oyipa kuti akupangitseni inu kusangalala ndi abwinowo. Inu mukuyenera kukhala ndi matenda pang'ono kuti akupangitseni inu kusangalala ndi thanzi labwino. Mukuona? Ndipo mukuyenera kukhala ndi zigwa zanu kuti zikupangitseni kusangalala ndi nzonga za mapiri. Ndipo kotero ndiye ena mwa masiku awa onse adzakhala nsonga ya phiri, izo zonse zidzakhala thanzi, izo zonse zidzakhala Mulungu, zonse zidzakhala chimwemwe, basi... padzakhala—padzakhala zimwemwe zosatha. Koma kufikira nthawi imeneyo, mwaona, ife tikuyenera kukhala ndi zabwino ndi zoyipa izi.

165 Tsopano, aliyense akumvetsa zimenezo, nenani “Ameni.” [Osonkhana akuti, “Ameni.”—Mkonzi.]

166 Mtsikana ameneyu ankanena kuti iye ankayesetsa kuti amupeze Mulungu kulikonse kumene ankapita. Iye amakhoza kupita ku mpingo *uwu* ndi mpingo *uwo*, ndi china chirichonse, koma iye sankakhoza kuchipeza Icho. Ndipo pamene iye anapeza, akuyenda chotsika mumsewu, panali Mwamuna wamng’ono wokalamba akuyenda mumsewu, munthu wamng’ono, ndipo iye anali ndi tchalitchi chachikulu chonse pamsana pake. Iye anali kuyenda mumsewu. Ndipo iye anati, “Oh, Munthu wabwino!” Iye anati, “Mai, ndizo zabwino kwambiri za inu,” anati, “koma Inu—Inu—Inu muli nacho chinthu chonsecho pa nsana Wanu,” iye anati, “icho, chikuphwanyani Inu.”

Iye anati, “Ayi sichindiphwanya Ine,” anati, “pakuti Ine ndine Thanthwe limene icho chinamangidwapo.” Ndi Iyeyo.

Tiyeni tipemphere:

167 O Thanthwe la Mibadwo, ndine wokondwa kuti ndangokwera mu tchalitchi, podziwa kuti ife tikupumula pa Thanthwe. Oh, Iye anati, Thanthwe, “Palibe kuposa pepala.” Ndipo pamene Thanthwelo linayamba kuyenda mofulumira nalo, mabelu okongolawo anayamba kulira mkati. O Thanthwe la Mibadwo, tibiseni ife mu zifundo Zanu. Tinyamuleni ife panjira ndi mtsinje wa moyo kuti mitima yathu ikhale yodzala ndi chimwemwe ndi kulira matamando kwa Inu mu njira yonse.

168 Ife tikukuthokozani Inu chifukwa cha kutichezera uku mmawa uno kwa Mzimu Woyera mu Mawu, pamene Iwo umabwera mkati ndi kuwapangitsa Mawu kukhala enieni kwambiri kwa ife. Tikhululukireni ife zolakwa zathu ndi zonse zomwe tachita kapena kunena zomwe zinali zolakwika, tikhululukireni ife chifukwa cha izo. Tithandizeni ife kuti tikhale Akhristu abwinoko, Atate Mulungu. Ife tikupemphera kuti chifundo Chanu chikhale pa ife.

169 Ine ndikupempha, Ambuye, ngati icho chiri chifuniro Chanu, kuti ife tikhoze kubwereranso kachiwiri posachedwapa ndi—ndi kudzatsiriza mitu iyi apa ndi kutenga zisindikizo zisanu ndi ziwiri izi. Ife—ife tikuyembekezera nthawi imeneyo, Ambuye, kuti pamene Inu—Mudzatero—Inu mudzatilola ife kuchita izo. Ndipo, Atate, pomwe pano mu mpingo wathu wawung’ono womwe ife tikupemphera kuti Inu mupereke izo kwa ife, kuti ife tikakhoze kumvetsa zinthu zazikulu izi za Mulungu. Osati chifukwa choti ife tikuyenera izo, Ambuye, koma mitima yathu yanjala ikuwukha magazi chifukwa cha izo. Ife tikupemphera kuti Inu mupereke izo.

170 Ife tikumupempherera M’bale wathu Neville, Ambuye, m’busa wathu wokhulupirika wotumizidwa ndi Mulungu. Ife tikumupempherera iye kuti Inu mumuthandize iye ndi

kumudalitsa iye, iye ndi mkazi wake wamng'ono wokoma, kanthu kakang'ono kokongola, ndi ana ake aang'ono.

<sup>171</sup> Ife tikupempherera matrastii onse ndi madikoni ndi aliyense amene amabwera ku mpingo uno. Osati wathu wokha, komanso wa ena ndi onse amene amayitanira pa Dzina lanu. Ine ndikupempherera anzanga ochokera ku dziko lonse, basi kungodzidzimutsidwa ndipo apa iwo ali. Atate, ine—ine ndikungokuthokozani Inu chifukwa cha izi.

<sup>172</sup> Ine ndikupemphera kuti Inu mufulumizitse tsikulo kuti pamene Yesu adzabwera ndipo ife tonse tidzasonkhanitsidwa pamodzi kumene sikudzakhala usana kapena usiku, ngakhalenso nthawi, izo zidzalumikizana mu Umuyaya ndipo kumene tonse tingadzakhale pamodzi kwamuyaya. Perekani izi, Ambuye.

<sup>173</sup> Ndipo ngati alipo ena pano mmawa uno, Ambuye, amene samakudziwani Inu ngati Mpulumutsi wawo, mulole iwo afune kuti amudziwe Mwanawankhosa uyu Amene wagwira Bukhu lachinsinsi la zisindikizo zisanu ndi ziwiri mu Dzanja Lake. Mulungu, mulole ife tikhale omudziwa Iye kotero mtsogolomu pamene ife tidzawona zisindikizo izo zikutsegulidwa ndiye ife tikhoza kuwona chimene Mulungu akuyankhula kwa ife. Ife tikupempha izi kwa ulemerero wa Mulungu, kudzera mu Dzina la Mwana Wake, Yesu Khristu.

Ndipo mitu yathu ili chiweramitsire:

<sup>174</sup> Kodi pangakhale wina akuti, “Ndikumbukireni ine, M'bale Branham, pamene inu mukupemphera, ndipo ndikufuna kuti ndikumbukiridwe mu pemphero?” Mulungu akudalitseni inu. Mulungu akudalitseni inu. Ndipo Mulungu akudalitseni inu, ndi inu, ndi inu. Inde. Mulungu akhale wabwino kwa inu. Inde. Mwinamwake manja ma dazeni awiri, kapena kupitirira, mmwamba.

<sup>175</sup> O Ambuye, Inu mukuwaona manja awo, Inu mukudziwa zokhumba zawo. Inu mukudziwa zomwe ziri mmitima mwawo, ine sindikudziwa. Ine ndikupemphera kuti Inu muwululire kwa iwo, Ambuye, ubwino Wanu ndi chifundo Chanu. Akhululukireni iwo pa chirichonse. Ngati ali matenda, Ambuye, chiritsani matupi awo ndi kuwapanga iwo kukhala bwino. Chitani Atate, pamene kudzoza kwa Mzimu Woyera kuli pa msonkhano, pa osonkhana tsopano. Mulole Mulungu wamkulu wa Kumwamba angodzozo kotero kuti Iye adalitse ali yense mu Kukhalapo Kwauzimu, kuti ife tikhoze kuchoka pano mmawa uno, tikunena, “Kodi mitima yathu siinantenthe mkati mwathu?” Perekani izi, Ambuye.


<sup>176</sup> Tsopano, ine ndafooka ndi kutopa, liwu langa lapita, ndipo ine—ine ndikungopempherera, Mulungu, chifukwa cha mphamvu zanga zomwe. Kodi Inu mungandithandize ine? Kodi Inu mungandilimbitse ine? Gwirani bala laling'ono ilo panso



apo, Ambuye. Kodi Inu mungatero? Mulole Mafuta Oyera a Mulungu asunthire mmenemo, ndi kulowa mu bala lina lirilonse, Ambuye, kulikonse kwa aliyense. Ife tikufuna kuti tikhale moyo, Ambuye, kwa ulemu Wanu ndi ulemerero Wanu. Perekani izi. Ndi kuchiritsa odwala onse ndi osautsika. Ndi—ndi kudzitengera ulemerero kwa Inueni, Ambuye, chifukwa ife tikuzindikira kuti sipatenga nthawi yayitali mpaka ife. . .ife sitidzakhhalanso ndi misonkhano iyi; iyo idzakhala itapita, iyo idzakhala nthawi yakale.

<sup>177</sup> Tsopano, Atate, dalitsani, tsopano, ife tikupempha tonse palimodzi kudzera mu Dzina la Yesu Khristu.

<sup>178</sup> Ndiyeno, Atate, ife tikupemphanso kuti Inu muwakumbukire iwo amene ati abatizidwe mmawa uno mu Dzina la Ambuye Yesu, kuti Inu muwapatse iwo ubatizo wa Mzimu Woyera, ulemerero wawukulu ndi ulemu. Perekani izi, Atate. Ife tikuzipereka izo zonse kwa Inu tsopano.

<sup>179</sup> Ndipo, Atate, ndi zonse izo, ine ndikudziponyera ndekha mkati. Musandiyiwale ine, Ambuye, mungondithandiza ine tsopano. Ine ndikupemphera mu Dzina la Yesu. Amen. 

61-0611 Chibvumbulutso, Mutu Faivi Gawo I  
Branham Tabernacle  
Jeffersonville, Indiana U.S.A.

CHICHEWA

©2024 VGR, ALL RIGHTS RESERVED

VOICE OF GOD RECORDINGS, MALAWI OFFICE  
P.O. BOX 51453, LIMBE, MALAWI

VOICE OF GOD RECORDINGS  
P.O. BOX 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.  
[www.branham.org](http://www.branham.org)

## Chidziwitso kwa ofuna kusindikiza

Maufulu onse ndi osungidwa. Bukhu ili mukhoza ku printa kunyumba kwanu ngati mutafuna kuti mugwiritse ntchito inuyo kapena kuti mukawapatse ena, ulere, ngati chida chofalitsira Uthenga wa Yesu Khristu. Bukhu ili simungathe kuligulitsa, kulichulukitsa kuti akhalepo ambiri, kuikidwa pa intaneti, kukaliika pakuti ena azitengapo, kumasuliridwa mu zinenero zina, kapena kugwiritsidwa ntchito ngati njira yopezera ndalama popanda chilolezo chochita kulembedwa ndi a Voice Of God Recordings®.

Ngati mukufuna kuti mumve zambiri kapena ngati mukufuna zipangizo zina zimene tiri nazo, chonde mulembere ku:

VOICE OF GOD RECORDINGS, MALAWI OFFICE  
P.O. Box 51453, LIMBE, MALAWI

VOICE OF GOD RECORDINGS  
P.O. Box 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.  
[www.branham.org](http://www.branham.org)